

YESU KHRISTU YEMWEYO

DZULO, LERO, NDI

KWANTHAWIZONSE



Zikomo inu, m'bale. [M'bale Samuel Johnson akuti, "Mulungu akudalitseni inu, M'bale Branham."—Mkonzi]. Mai, ine ndingakonde ntamakhala nayo ina, kuti ndizikhala ndi mbiri ngati imeneyo, sichoncho ine? Ine ndithudi ndikuyamikira zimenezo, chonchobe. Ngati pakanakhala kuti panalibe aliyense wokhulupirira, zikanandichitira ubwino wanji kuti ndipite? Eya. Iwe umayenera kukhala ndi winawake woti akhulupirire. Ziribe kanthu zomwe Mulungu angachite, ngati inu simukhulupirira zomwe Iye akuchita, ndiye... Zikuyenera kukhala awiri a ife, inu mukudziwa, winawake akuyenera kukhulupirira ndi ine chifukwa cha izi. Ndipo ziribe kanthu zimene zingachitike, ngati—ngati sipakhala woti akhulupirire, ndiye izo zingakhale zopanda phindu, izo sizingakhale ndi ntchito nkomwe. Koma ndine wokondwa kwambiri kumva kuti anthu akukhulupirirabe nkhani yodabwitsa iyi ya Ambuye Yesu. Iye ndi chifundo cha chikondi kwa ife tonse.

² Ndipo ine ndinali ndi nthawi yopambana chotero usiku wathawu. Ine—ine ndinapita kunyumba ndipo ndikukhalabe moyo pa zotsatira za izo mpaka nthawi ino. Ine ndabwereranso kuti ndidzadzazitse. Ndipo ine ndikuganiza kuti ichi ndi chimene ife tonse tabwerera, ndi kudzamva nyimbo za Zion, maumboni a anthu, ndipo mnyumba ya Ambuye.

³ Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti zinanenedwapo kamodzi, mu Baibulo, "Ndi zokoma bwanji kuti abale azikhala limodzi mu umodzi." Ziri ngati mafuta odzozera omwe anali pa ndevu za Aroni, omwe ankayenderera mpaka ku mphonje za mkanjo wake. Ine ndikuganiza kuti palibe chirichonse chofunika kwambiri kuposa kuwona—anthu ogwirizana, mu Mzimu wa Ambuye, kuti pakhale umodzi, onse kumagwirizana.

⁴ Inu mukudziwa, ine ndikuganiza kuti masiku teni amene iwo ankawuyembekezera—wapachiyambi, kutsanulira koyamba kwa Mzimu Woyera, momwe iyo ikuyenera kuti inali nthawi yogwirizana, ya anthu onse mwa mtima umodzi ndi cholinga chimodzi. Ndipo nthawi iliyonse imene anthu asonkhana pamodzi monga choncho, kuyambira pamenepo, Mzimu Woyera nthawizonse umakumana ndi iwo.

⁵ Baibulo linati, Yesu akuyankhula, ananena kuti, "Paliponse

pamene awiri kapena atatu asonkhana mu Dzina Langa, pamenepo Ine ndiri pakati pawo.” Koterotsopano ife tikudziwa, moona, kuti Yesu wasonkhana ndi ife, chifukwa ife tasonkhana mu Dzina Lake.

⁶ Tsopano, usikuuno, waperekedwa kuti tipempherere anthu odwala. Ndipo pamene ine ndimalowa pakhomo, ine ndinawona kuti panali iwo atagona pamenepo, amene anali odwala ndi osautsika. Mwana wanga anali atangobwerera kumene kokamutenga Mlongo Moore ndi ine, ndi kutibweretsa ife ku tchalitchi; ndipo iye anati anali atapereka makadi ena a pemphero, koterotso kuto kuti iye akhoze kuwawerenga iwo ndi—ndi kuwabweretsa anthuwo mmodzi pa nthawi, kuti tiwapempherere iwo.

⁷ Lero ine ndinali ndi tsiku lopambana. Ine ndinali kumusi pa—pa bwalo laling’ono kumusi kuno, ndipo apo panali munthu akubwera, akusonkhanitsa—zinthu kuchokera mu chidebe cha zinyalala.

Ine ndinati, “Ine ndabwera kuno chifukwa cha msonkhano.”

Iye anati, “Oh, kumtunda uko ku bwalo la msasa?”

Ine ndinati, “Inde.”

⁸ Iye anati, “Chabwino,” iye anati, “Ine ndipita uko mawa usiku.” Iye anati, “Kuli mtumiki, M’bale Branham, akukayankhula.”

Ndipo ine ndinati, “Inde, bwana.”

⁹ Ndipo iye anati, “Chabwino,” iye anati, “Ine ndikufuna kuti ndipite kumeneko.” Anati, “Mkazi wanga ndi banja anali kumeneko usiku wathawu.” Ndipo—ndipo a—bamboyo anali akusuta.

¹⁰ Ndipo—ndipo ine ndinati, “Chabwino,” ine ndinati, “kodi inu mumamudziwa M’bale Branham?”

¹¹ Anati, “Oh, zakhala ziri zaka zapitazo.” Anati, “Iye anali kuno kwa... Ine nthawizonse ndinkaganiza kuti izo zimatengera kulimba mtima kochulukuka, kapena chikhulupiriro, kapena chinachake.” Anati, “Ine ndinali cha kuno ku bwalo la zida zankhondo kuti ndidzamuwone iye akuwabweretsa anthu amenewo uko, pa mabedi ndi machira, ndi akhungu ndi olumala, ndi kuwawona iwo akuyenda kuchoka pa nsanja.”

Koma ine—ine ndinati, “Ine—ndine M’bale Branham.”

¹² Ndipo iye—iye anati, “Oh, ine sindiri... ” Anakhala ngati akuyika ndudu yake kumbuyo. Ndipo mtundu wa njonda ya munthu. Ndipo mwamuna wina anabwerapo, wabwino kwambiri.

¹³ Ife tinali ndi kuyankhulana pang’ono, ndinkafotokoza kwa iwo za Kukhalapo kwa Mulungu. “Pali—palibe—paliponse pamene inu mungayang’anepo. Inu mukhoza kuyang’ana pa

mtengo, inu mukhoza kuwona kuti iwo ukulamuliridwa ndi Mulungu. Ndipo chirichonse chimene inu mumayang'anapo ndi Mulungu." Ine ndinati, "Ine ndikuyembekeza kuti ngati ife titi tidzakomanenso, mu moyo, kuti inu mudzakhale Mkhristu monga banja lanulo." Ndinawapempherera iwo mwamsanga pamene iwo ankachoka, njonda yinayo.

¹⁴ Ndipo ngati iwo ali pano usikuuno, ine ndikuyembekeza kuti sindikuwachititsa iwo manyazi ponena izi, koma ine—ine—ine ndikudalira kuti Mulungu apanga Akhristu kuchokera mwa amuna awiri amenewo. Ife tikufuna kuti tidzakomanenso mu dziko labwinoko, kumene Mtengo wa Moyo ukuphukira kumbali inayo ya mtsinje. Ife tonse tikudziwa kuti tikubwera njira imeneyo.

¹⁵ Ndipo tsopano pomadutsa mmisika ndi malo, ndipo zimabweretsa zikumbutso zakale. Ndipo usiku watha pamene ine ndimatuluka, M'bale Johnson anali atakhala kunjira uko, m'bale, iye ndi Mlongo Johnson. Ine sindinawawone iwo kwa zaka zingapo. Nthawi yotsiriza imene ine ndinamuwona iye, iye anali atafa ziwalo, atapuwala. Kunali uko ku California, M'bale Noel. Izo zikubweretsanso zikumbutso za masiku akale, kubwera koyamba ku Arkansas, mzinda wawung'ono wotchedwa Moark, mpingo wawung'ono wa Chipentekoste utakhala uko kumbali imodzi. Mpaka mmusi kwa M'bale... ku Corning, Arkansas, M'bale Johnson ndi mkazi wake. Ndipo momwe ine ndikukumbukirira masiku opambana amenewo!

¹⁶ Kenako mpaka mmusi kwa M'bale T. Richard Reed. Ine ndikukumbukira mmawa, kumusi ku Jonesboro, mkazi wake, anali wosabereka. Iye ankafuna ana.

¹⁷ Ine ndinali kumbuyo uko mchipinda, ndipo anthuwo anali atang'amba chotchinga pa zenera, akulowa mkati, ndikupempherera odwala. Iye anandibwezera mchipinda. Ndimakhala ndi mzere wa pemphero. Iye ankaganiza kuti ndinalowa ndi kukagona, ndipo uko kumakhala anthu atayima mmwamba-ndi-pansi kubwalo la kuseri, akukhala ndi mzere wa pemphero. Ndipo iye ali kunjira uko akugona; ine ndinali kumbuyo uko ndikupempherera odwala, kudzera pa zenera.

¹⁸ Ndipo ine ndikukumbukira, mmawa wotsatira, ndikutuluka. Ndipo Mlongo Reed anali atathandizidwa ndi a dokotala ndi chirichonse, kuyesetsa kuti akhale ndi mwana. Ndipo ine ndinayamba kuyenda kudutsa pa zitseko, amodzi a masomphenya oyambirira mu msonkhano, ine ndinamuwona iye atanyamula khanda lalimuna la mutu wa mzindo. Ine ndinayankhula mu Dzina la Ambuye kuti iye akhala naye iye. Iye anatero, ndipo momwe Mulungu anadalitsira nyumba yawo.

¹⁹ Ndipo, oh, zinthu zambiri! Ndi M'bale G. H. Brown; Little Rock kumusi kuno. Ine ndikukumbukira kumeneko, 505 Victor Street.

²⁰ Inu mukudziwa, ine—ine ndikufuna kudzangotenga misonkhano ingapo ndi kudzabwereranso modutsa, mu Arkansas ndi mipingo imeneyo ndi zinthu, ndi kudzawawona anthu, ndi kudzagwirana nawo chanza. Ndizo zopambana, anthu a Mulungu! Kulikonse kumene ine ndapitako, ine ndakhalako komwe ku nkhalango za Afrika, ndi uko pakati pa Amwenye, odyamoto, ndi asing'anga, ndi konse kudutsa mmawu, ndi kuzungulira dziko lapansi, koma sindinaiwale konse azimzanga a ku Arkansas, momwe iwo ankagwirira manja amenewo, ndi kuwagoneka ana awo panso pa galimoto pamene iyo inali ikuimba. . . ikuvumba. Kuwaona atsikana achichepere akuyenda mumsewu, opanda nsapato, kapena akutsika mu msewu, ndipo kenako nkudzasasa fumbi pa mapazi awo ndi kuvala nsapato zawo ndi masokosi, nkumalowa mkati. Ine ndiri kumbuyo uko mu tchire, ndikupempherera msonkhano. Ine sindidzaiwala konse zimenezo, momwe iwo aliri anthu enieni. Ine . . . ndikungothokoza kwambiri kuti akadalipobe anthu onga amenewo mdziko.

²¹ Usikuuno, ine ndinaiwala za kubwera ku msonkhano uno tsiku lina, ndipo ndinangokokedwa, kukoka. Tsiku lina a . . . mmodzi wa mamenjala a msonkhano amene amasalira makalata akunja, anadzabwera ndi—ndi kuitana kwa kunja sikisi handirede, ndipo zochuluka za izo zopempha; pambali pake, bukhu lokandapala *chomwecho*, mmiyezi sikisi yapitayi, labwera la mmadera. Ine ndikanakonda ndikanapita kwa aliyense wa iwo. Koma ine kawirikawiri ndimangoyesetsa kuti ndizipita komwe Ambuye akunditsogolera ine. Ine sindinayambe ndalolapo kuti misonkhano yanga izikhala yaikulu. Ine ndikadali munthu wamng'ono wakale yemwe uja amene anabwera pa nthawi ina. Sindisowa kukhala ndi ndalama iliyonse. Ine ndiribe madongosolo aakulu aliwonse oti azindithandizira. Ine sindimasowa ndalama iliyonse nkomwe. Ambuye amasalira zimenezo, monga Iye ankachitira poyambirira.

²² Kusiyana kokhako usikuuno, ine ndinali kuyambira nthawi imene ine ndinabwera ku Corning, Ine ndikukhulupirira ine ndinali ndi—thumba lobowoka, la suiti imene m'bale wanga anandipatsa ine. Mnyamata wachichepere, ndipo iye—iye anaying'amba iyo. Ndipo—ndipo ine. . . Ilo linali mbali ya dzanja lamanja, ndipo panang'ambika malo aakulu pamenepo. Mkazanga ndi ine tinapita ku sitolo ya teni-cent ndipo tinakagula zina mwa zigamba izi zomwe mumazisitirapo, inu mukudziwa, koma icho sichinkasitika pa thumba ili. Ichu chinkapitirira kumamatukapo. Ndipo ine ndinadzipezera ulusi ndipo ndinachisoka icho. Iyo siinali ntchito yabwino kwambiri. Ndinalibe chikhotho nthawi imeneyo, ndipo ndikukumbukira kuti ndinkayenera kugwira dzanja langa lamanja pamalo ong'ambika amenewo, ndi kumagwirana

chanza ndi abwenzi anga atumiki ndi dzanja langa lamanzere, kuwopetsa kuti ndisawonetse chikhotho chimenecho. Ndipo ine ndinkati, “Mundikhulukire chifukwa cha dzanja lamanzere, ilo layandikira ku mtima wanga.” Chabwino, ine ndiri ndi chikhotho chabwinoko usikuuno, koma ine ndikufunabe kuti inu muyandikire pafupi ndi mtima wanga. Inu mwakhala muli kumeneko nthawi yonse. Ine ndikuwakonda Ambuye Yesu basi monga ine ndinkachitira nthawi imeneyo.

²³ Ndipo ine ndakhalapo ndi mwayi woyankhula kwa anthu faivi handirede sauzande pa nthawi imodzi. Ine ndawonapo kuitanira kuguwa, kochuluka monga mbadwa sarte sauzande zama bulangeti zikupereka mitima yawo kwa Yesu Khristu pa nthawi imodzi, akuswera mafano awo pabwalo. Ndawonapo zozizwitsa twente-faivi sauzande zapamwamba zikuchitidwa mu nthawi ya mphindi imodzi, ndi pemphero limodzi, ku Durban, South Africa; kumene magalimoto okwana sikisitini ananyamula zikuku, mabedi ndi machira—machira amabwera akutsika mu msewu.

²⁴ Tsiku lotsatira, pamene Sidney Smith, ameya, anandiuza ine kuti ndipite; anandiyitana ine, anati, “Mupite ku chipindacho ndipo mukayang’ane cha ku Nyanja ya Indian kumeneko.” Ndipo uko iwo ankabwera kumeneko, mbadwa zimene zinali pa nkondo kwa wina ndi mzake; zitagona mmabedi ndi mmachira, zinthu zopangidwa kunyumba zomwe iwo anawabweretsera iwo, dzulo lake; ndipo apa iwo ankabwera kumbuyo kwa magalimoto sikisitini odzaza awa, akuyimba, “Kungo khulupirira! Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira.”

²⁵ Zimakupangitsa iwe kuganiza, “Chisomo chodabwitsa, kukoma kwakeko, chimene chinapulumsa wopanda pake wonga ine.” Kudziwa kuti ine ndiri mu chiyanjano ndi anthu oterowo, kuti ndizikhala pano pa dziko lapansi ndi ku Umuyaya, limodzi.

²⁶ Ine ndikuwutenga uwu kukhala mwayi waukulu, mu msonkhano wanu, kapena kuno mu msonkhano wanu waukulu. Ine ndalemekezedwa mwapamwamba kuti ndidzayankhule pa umodzi wa misonkhano yanu mawa, masana ine ndikuganiza ndi choncho, ndipo kuyambira thwelovu koloko mpaka hafu pasiti thwelovu, kapena chinachake monga choncho, mawa. Ambuye akalola, ine ndikufuna kuti ndidzakhale pano basi ndi Uthenga wawung’ono wophweka.

²⁷ Usikuuno tsopano, kuti tidzapempherere odwala. Ine sindi... Kudzoza kwa kupempherera odwala ndi... Ndi Mzimu womwewo, koma kudzoza kosiyana pamene mukupempherera odwala, kuposa mmene zimakhallira mwanjira iyi. Ine sindinadye chichereni cha lero. Ndipo ine ndabwera mchiphinda chino, ndikusala kudya, kupemphera. Ndipo—ndipo ine sindikufuna kuti ndizilalikira kuchitira kuti ndikhale pansa pa

kudzoza monga pamene abale anga otumikirawa, akamalalikira. Ine—ine ndikufuna kuti ndizimverera Kukhalapo kwa Ambuye pamene ine ndikupempherera odwala, chifukwa aliyense amene ine nditi ndimupempherere, usikuuno, ine—ine ndikufuna kuti izo zikhale, ine ndikufuna kuti iwo achiritsidwe. Ine—ine ndikufuna izo kwa ulemelero wa Mulungu, kuti—kuti Mulungu achiritse odwala. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Iye achita zimenezo.

²⁸ Kotero kuti tichite izi, ndipo ambiri a anthu inu mwinamwake simunakhalepo mu msonkhano, ndipo ambiri a inu simukuwudziwa utumikiwu. Ena a inu mukukumbukira pamene ine ndinali kuno nthawi yoyamba mu Arkansas. Izo zinanenedweratu, inu mukukumbukira. Ine ndinkagwira dzanja la anthu, ndipo ine ndinkangogwira dzanja lawo pamenepo kwa mphindi pang'ono, ndiye kenako Ambuye ankakhoza kuyankhula ndipo ankakhoza kungonena chimene iwo anali nacho. Kenako ine ndinadzakuuzani inu kuti Iye anandiuza ine, pamene Iye anakomana nane, kuti, “Iwe, ngati iwe utadzakhale woonamtima, kuti izo zidzawonjezerekanso ndipo iwe uzidzadziwa chinsinsi cha mitima yawo.” Ndi angati anayamba andimvapo ine ndikunena zimenezo izo zisanachitike? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino, izo zinafika kumeneko. Tsopano zawonjezereka. Izo zikungopitirira. . . Ambuye akungopitiriza kudalitsa, ndipo ife ndi othokoza basi chifukwa cha zimenezo.

²⁹ Mwanjira yina, ine si mlaliki; aliyense akudziwa zimenezo. Ndine, ndine—ndine tayara lapadera. Iwe umagwiritsa ntchito tayara lapadera pamene uli ndi. . . Ife tiribe akuphwa, ngakhalebe. Tsopano ife, ine ndinangopezeka kuti ndikubwera, ndipo iwo akungofuna kuti agudubuze lapaderalo kwa kanthawi pang'ono. Koma ine—ndine mtumiki wa tayara lapadera, chifukwa ine ndiribe maphunziro oti ndikhale mlaliki; sindinapiteko ku sukulu iliyonse ya Baibulo. Koma chimene ine ndikuchidziwa cha Yesu Khristu, ine ndimakonda kuchifotokoza icho mwanjira yanga yofooka, ndipo Mulungu amachilemekeza icho. Ndipo ine ndikuyembekeza, usikuuno, kuti mwanjira imene Iye ananditumizira ine kuti ndidzatumikire kwa anthu, imene ili kupempherera odwala, kuti Iye adzitsimikizira Yekha pamaso panu usikuuno, kuti Mulungu amene ine ndimamukonda ndipo inu mumamukonda ali ndi ife usikuuno.

³⁰ Tiyeni tsopano kwa Uthenga wawung'ono wa chizolowezi. Ngati iwe supereka Uthenga pamaso pa anthu, winawake samamvetsa. Iwo amachokapo ndi kumati, “Ine sindinayambe ndamvapo zoterozo. Ine ndikudziwa kuti palibe chinthu choterocho mu Baibulo.”

³¹ Chotero kuti tithe ku—kuti tiziyale izi pansi, ine—ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwatcheru kwenikweni tsopano, kwa mphindi pang'ono, za mutu wa Uthenga

wachizolowezi wawung'ono, mutu wa msonkhano: *Yesu Khristu Yemweyo Dzulo, Lero, Ndi Kwanthawizonse*. Tsopano mukumbukire mutu umenewo, kuti: *Yesu Khristu Yemweyo Dzulo, Lero, Ndi Kwanthawizonse*.

³² Ndipo ine ndikufuna kuti ndifunse ichi, ine ndisanawerenge, kodi inu mukundimva ine bwino bwino? Winawake anandiuza ine kuti zikuphokosera, chifukwa siling'i ili monga choncho. Kodi ziri bwino ine ndikayima mmbuyo monga *chonchi*? Kodi ndi choncho? [Osonkhana akuti, "Ayi."—Mkonzi]. Ayi. Ndikuyenera kuti ndiyandikire. Kodi ziri bwino? ["Inde."] Chabwino. Izo ziri bwino. Chabwino.

³³ Tsopano ife tikufuna kuti titsegule mu Malemba, ku Yohane Woyera 12, ndi ndime ya 20, ndipo tiwerenge kuchokera apa.

Tsopano panali Agriki ena pakati pawo amene anabwera kudzapembedza pa phwando:

Omwewo anabwera kotero kwa Filipino, yemwe anali waku Bethsaida waku Galileya, ndipo anamupempha iye, kuti, Bwana, ife tikufuna kumuwona Yesu.

³⁴ Tsopano limenelo ndi funso ndithudi, ndipo icho ndi chokhumba chachikulu. Ndipo tsopano, kwa maminiti twente kapena sarte otsatirawa, tiyeni timvetsere mwatcheru kwenikweni tsopano, ndiyeno icho sichikhala chinsinsi kwa inu.

³⁵ Tsopano, ine ndi wokhulupirira wamkulu mu chimene Mawu a Mulungu amanena. Tsopano, ine ndikudziwa kuti Mulungu akhoza kuchita zinthu zimene sizinalembedwe mu Mawu. Koma ali . . . ngati Iye ati angochita chimene Iye analonjeza mu Mawu, izo zikhala zokwanira kwa ine, kuti ndingomuwona Iye. Ndiye ine ndikudziwa kuti izo ndi zolondola, ngati Iye analemba izo mu Mawu.

³⁶ Tsopano ngati Baibulo linanena kuti, "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse," tsopano Agriki awa anali ndi chikhumbo chomwecho, ine ndikuganiza, chimene ife tonse tiri nacho pano usikuuno. Pakuti, palibe mwamuna, kapena munthu, amene anayamba walimvapo Dzina la Yesu Khristu, koma amene amakhala ndi chikhumbo chomuwona Iye.

³⁷ Ngati ine ndingawafunse omvetsera awa usikuuno, ine ndikuganiza kuti dzanja lirilonse lingapite mmwamba, "Kodi inu mungafune kumuwona Yesu?" Ndizo basi, mwaona, paliponse. Ife timamukonda Iye. Chabwino, ndiye ine ndikufunsa funso ili, ndiye chifukwa chiyani sitimamuwona Iye, ngati Baibulo linati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse?

³⁸ Tsopano izo sizimatanthauza basi mwanjira yatheka. Baibulo linati, "Iye ali yemweyo." Tsopano kwa ine, Baibulo ndi . . . mwina Ilo likulakwitsa kapena Ilo likulondola. Tsopano,

ngati amenewo si Mawu odzozedwa a Mulungu, ndiye ine sindikudziwa choti ndikhulupirire.

³⁹ Ine ndakhalapo ndi mwayi woona ambiri, mawonekedwe ambiri a chipembedzo, mu—mu—mu Durban momwe.

⁴⁰ Ndipo mu Bombay, ine ndinasangalatsidwa masana ena mu kachisi wa ma Jains, kumene zipembedzo seventini zosiyanasiyana za ku India, chirichonse cha izo chikumukana Yesu Khristu, ndi chirichonse. . . Ndinasangalatsidwa kumeneko ndi zipembedzo seventini zosiyanasiyana izi.

⁴¹ Ndipo ine ndinawona usiku umenewo, pansi pa mphamvu ya Mzimu Woyera, momwe Mulungu anamubetchera munthu woyera aliyense, chipembedzo chirichonse, ndi china chirichonse, kwa munthu wakhungu atayima pa nsanja. Pamene iwo anawona kuzindikira za mumtima, iwo ankaganiza kuti kunali kuwerenga maganizo kwa mtundu winawake. Kenako masomphenya anawonekera a munthu amene anali wakhungu kwa zaka twente, wopembedza dzuwa. Ndipo ine ndinawona mmasomphenya kuti iye anali woti achiritsidwa. Kenako ine ndinamubetchera wansembe wa Chimuhamedi aliyense, wansembe wa Chibuddha aliyense, munthu woyera aliyense, achi Raja, onse, kuti, “Munthu aliyense amene angabwere pano ndi kudzamupatsa munthu uyu kupenya kwake, ine ndimupembedza mulungu amene angamupatse iye kupenya kwake. Ndipo iye anati akanachita chimodzimidzi.” Iye ankapembedza dzuwa.

⁴² Ndipo ine ndinati, “Chiyani, kodi inu mungachite chiyani? Kodi inu Achimuhamedi mungachite naye chiyani iye? Inu mungati, ‘Iye amapembedza—chirengedwe mmalo mwa Mlengi.’” Ine ndinati, “Ine ndingati ‘ameni’ kwa zimenezo. Komano pakuyenera kukhala winawake akulondola ndi winawake akulakwitsa.” Ine ndinati, “Inu mungachite chiyani? Inu mungampange iye kukhala wa Chimuhamedi. A Buddha angampange wopembedza Buddha, ndi zina zotero.” Ine ndinati, “Inu mungachite chiyani? Inu mungakhoze kungosintha malingaliro ake. Inu mungakhoze kungosintha njira yake ya kaganizidwe.”

⁴³ Ine ndinati, “Ife tiri ndi chinthu chomwecho mu United States. Amethodisti onse amafuna Abaptisti kuti akhale Amethodisti. Ndiyeno Apresbateria amafuna iwo onse kuti akhale Achipresbateria. Ndipo—ndipo a Oneness amafuna kuti iwo akhale a Twoness. Ndipo a twoness amafuna kuti iwo akhale. . . Oh, mai! Ndi chiyani chimenecho? Ndi kusintha kwa malingaliro. Pakuyenera kukhala chinachake chenicheni penapake. Mwaona, chinachake chikuyenera kukhala cholondola, ndipo chinachake ndi cholakwika.”

⁴⁴ Ine ndinati, “Tsopano mulole Mulungu wa chirengedwe abwezeretse kupenya kwake, pamaso pa anthu theka la millioni.

Ndipo iye anati, mulungu amene angamupatse iye kupenya kwake, iye adzamutumikira.” Ndipo ine ndinati, “Ine ndikhala wophunzira wa munthu amene ati abwere ndi kudzamupatsa iye kupenya kwake.”

⁴⁵ Awo anali achete kwambiri faivi handiredi sauzande amene inu munayamba mwawamvapo. Panalibe. Ine sindikanapanga kubetchera kumeneko ndikanapanda kuwona masomphenyawo. Tsopano, apo panali mboni faivi handiredi sauzande za izo.

⁴⁶ Ndipo ine ndinati, “Bwanji inu simukubwera? Chifukwa inu simungathe kuchita zimenezo.” Ndipo ine ndinati, “Inu, inu Achimuhamedi, inu mumanena kuti chipembedzo cha Muhamadi ndi chachikulu kwambiri mu fukoli,” ndipo ine ndinati, “ndipo izo zikhoza kukhala, mu chiwerengero; ndi a Buddha, ndi ena otero. Koma ndithudi pali wansembe wina amene ali wokhoza kubwera ndi kudzatenga kubetchera uku.” Palibe amene anatero.

⁴⁷ Ine ndinati, “Chifukwa chimene inu simukutero, ndi chifukwa chakuti inu simungathe. Ndipo ngakhalenso ine sindingathe. Koma Mulungu wa Kumwamba, anamuukitsa Yesu Khristu, Amene ine ndiri mboni Yake usikuuno, kuti ndawona masomphenya kuti munthuyo alandira kupenya kwake. Ngati iye sachita zimenezo, ndiye ndine mneneri wabodza, ndipo mundithamangitse ine mu dera lanulino. Koma ngati Iye achite zimenezo, ndiye ndinu okakamizika, pamaso pa ansembe anu omwe ndi chirichonse, kuchitira umboni kuti Iye ndi moona Mwana wa Mulungu, ndi Mpulumutsi wa dziko lapansi.” Aliyense anali chete.

⁴⁸ Anamubweretsa munthu wakhunguyo; ndinayika mikono yanga momukumbatira iye. Ine ndinati, “Ambuye Yesu, molingana ndi masomphenya amene sangalephere, ine ndikupemphera kuti Inu mumupatse munthuyo kupenya kwake.” Ndipo iye anayamba kufuula. Ndipo ameya a mzindawo anali atakhala pamenepo, ndipo anathamanga ndipo anakamugwira iye. Iye amakhoza kupenya bwinobwino momwe ine ndimachitira.

⁴⁹ Ndiye iwo anali ndi asilikari pafupifupi, oh, mahandiredi a asilikali, amalephera kuti awabweze anthuwo mmbuyo. Iwo amathamanga pamwamba pa asilikaliwo, amathamanga panso pa miyendo yawo ndi ndodo, zimene iwo ankagwiritsa ntchito pothamangitsira khamulo mmbuyo. Nthawi yomwe ndimadzafika pa galimoto ndi kutuluka, ine ndinat sala pang’ono kukhala wopanda zovala, wopanda nsapato kumapazi anga, akugwedeza kufuna nsapato, ndi kugwedeza kufuna chikhotho ndi chirichonse, akuchita njala ndi ludzu la Mulungu.

⁵⁰ Koma Mulungu wa Eliya akadali moyo lero, ndipo Iye ali Mulungu mochuluka basi monga Iye anali nthawizonse.

⁵¹ Tsopano oyambitsa onse a chipembedzo. Atayima pamenepo pa manda a Muhamadi, pakhala pali kavalo woyera, yemwe wakhala akuyima pamenepo kwa zaka thuu sauzande. Iwo akhala akusinthazila azilonda pafupifupi maora foro kapena sikisi aliwonse, ndipo iwo akuyembekezera kuti Muhamadi adzawuka ndi—ndi kudzazungulira dziko lonse. Inu mukudziwa, a... ndipo iye analemba bukhu la Korani, ndi zina zotero. Koma, oh, Buddha, pafupifupi zaka twente-firii handiredere zapitazo, anali m—munthu, munthu wachipembedzo mu—mu Japan, ndi zina zotero. Ndipo zipembedzo zonsezi, mmodzi aliyense wa woyambitsa wawo anafa ndipo ali mmanda.

⁵² Koma Chikristu, pambuyo pa chochitika-chapadziko lapansi lonse, Chikristu ndi chipembedzo choona chokhacho. Ndi chokhacho chimene chingawonetse manda opanda kanthu. Ndi chimodzi chokhacho chimene woyambitsa wawo, munthu aliyense, ndipo palibe munthu wonga Iye, amene anayamba wayimapo pa dziko lapansi nkudzati, “Ine ndiri ndi mphamvu yosiya moyo Wanga pansa ndi kuwutenganso iwo kachiwiri. Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwanonso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine. Wosakhulupirira sadzandiwanonso Ine, komabe inu mudzandiwona Ine. Pakuti Ine,” Ine ndi mlowammalo waumwini, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumalekezero a dziko lapansi, mpaka ku chimaliziro.” Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse!

⁵³ Tsopano ife tikufika ku lingalirolo. Tsopano ngati Iye ali yemweyo, Iye si wakufa. Iye anawuka kwa akufa, ndipo Iye analonjeza kuti okhulupirira Ake akanadzamuwona Iye, njira yonse mpaka kumapeto. Mpaka ku chimaliziro, kuti iwo akanati adzamuwone Iye, tsopano, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

⁵⁴ Anthu ambiri amene ine ndayankhulapo nawo, anati, “Chabwino, mwa njira ina Iye ali yemweyo.”

Baibulo silinati, “mwanjira inayake.” Ilo linati, “Iye ali yemweyo.”

⁵⁵ Ndipo ngati ife tikuchita njala kuti timuwone Iye, ndi chidwi chomwecho chimene Agriki awa anali nacho. Iwo anali atamva za Iye, iwo anabwera ndipo anafika kuti adzamuwone Iye, kudzera mu kukoma mtima kwa mmodzi wa ophunzira Ake. Chabwino, kodi ife sitingachite chimodzimodzi, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.”

⁵⁶ Tsopano, ife tikhoza kuyankhula za chiwukitsiro, ife tikhoza kuyankhula za icho. Koma ngati icho sichiri chenicheni, icho chimangokhala chabe—nthano chabe, ndi nkhani. Koma ngati icho chatsimikiziridwa kuti ndi Choonadi, ndiye ife tiri pakati

pa anthu okondwa kwambiri, ndipo ndine wokondwa kukhala ndi iwo.

⁵⁷ Tsopano, ngati—ngati Yesu Khristu ati awonekere pamaso pathu, usikuuno, ndipo ife nkukhoza kuwona pogwiritsa ntchito mfundo zoperekedwa ndi Mulungu, ndi mwa machitidwe omwewo a Umunthu Wake, kuti Iye ali pano, ndiye ife tikuyenera kumulandirako Iye, kumupanga Iye kukhala wolandiridwa. Tsopano, ilo ndi neno lalikulu kwambiri, koma ife tiri ndi Mulungu wamkulu kwambiri amene amasunga aliwonse a Mawu Ake.

⁵⁸ Ndipo pamene ife tipeza chirichonse mu Baibulo, mudzipachika solo yanu pa chimenecho. Icho ndi Choonadi. Muzingokhala ndi chimene Mulungu analonjeza, Mulungu adzachichita.

⁵⁹ Ngati ife tiri ana a Abrahamu, ife timakhulupirira zinthu zimenezo. Abrahamu, motsutsana ndi zochitika zazikulu, anazitcha zinthu zimene kunalibe, ngati kuti zinalipo, chifukwa iye anakhulupirira kuti Mulungu anali wokhoza kusunga Mawu Ake. Ndipo ife timadzitcha tokha ana a Abrahamu. Abrahamu anadikirira kwa zaka twente-faivi ku lonjezolo. Mmalo momafookera, iye anakulirabe mwamphamvu. Ndipo ndi mosiyana bwanji ndi momwe zikukhalira lero ndi Mbewu Yake yachifumu.

⁶⁰ Tsopano, mbewu yeniyeni ya Abrahamu ndi—anali Isaki, ife tikuzindikira zimenezo, amene anabwera monga Myuda, amene ali mwathupi.

⁶¹ Koma Mbewu imene Mulungu ankaiperekerera lonjezo, inali Mbewu ya Abrahamu, chikhulupiriro chimene iye anali nacho mwa Mulungu. Chimene, kudzera mwa Yesu Khristu, Amene ali Mawu Ake, ife timakhala olandira limodzi ndi Iye. Ndipo mpingo uno, usikuuno, wa amwendamnjira a tsiku lino, ndi mwamtheradi Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ndi chikhulupiriro chenicheni.

⁶² Tsopano, ngati ndingat ndiwafunse Amethodisti, “Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?” “Inde.” “Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye ali ndi inu?” “Inde.” Abaptisti, Apresbateria, Achilutera, Achipentekoste, ena otero, aliyense anganene chimodzimodzi.

⁶³ Koma tsopano kodi ife tingamufunefune chotani Iye? Ndi munthu wa mtundu wanji amene ife tingamamufunefune, ngati ife titafuna kuti tiwone ngati Iye anali yemweyo? Ngati Iye akanakhala kuno mu Arkansas, usikuuno, mu kachisi uno, kodi ife tingamafunefune munthu wa mtundu wanji?

⁶⁴ Ife, ife tingamafunefune winawake amene ali, chabwino, mwinawake wovala mkanjo wautali, ndi ndevu pa nkhope yake, ndi zipsyera za misomali mdzanja lake, ndi zipsyera za minga pa—pa chipumi chake? Ngati inu mungamayang’ane

munthu wonga ameneyo, wachinyengo aliyense akhoza kukunyangani inu pa zimenezo. Ndiko kulondola, kutsanzira. Munthu akhoza kujambula zipsyera m’manja mwake, ndipo akhoza ngakhale kudzibaya yekha ndi minga ndi kupanga zipsyera, koma wotsanzira aliyense akhoza kuchita zimenezo.

⁶⁵ Komano ndiye ngati ife sitimayembekezera munthu wa mtundu umenewo, osati chifukwa cha mavalidwe ake kapena momwe thunthu lake linali. Chifukwa, ngati Iye atati ali pano, Iye angavale munga momwe ife tikualiram. Panalibe kusiyana kulikonse. Iye ankavala ndipo ankayenda pakati pa anthu basi momwe anthu ankachitira. Iye sankavala konse munga m’busa wa tsiku limenelo. Iye ankangovala chovala wamba cha mu msewu. Chotero Iye angangovala mwawamba, mwinamwake atavala suti, ndi zina zotero, munga momwe munthu wina aliyense lero angavalire. Munga munthu wogwira ntchito, kapena a—munthu wamalonda, kapena china chirichonse, umo ndi momwe Iye angamavalire. Kotero inu simungamudziwe konse Iye mwanjira imeneyo. Inu simungamudziwe konse Iye mwa thunthu la kawonekedwe, kaya Iye anali wamtali, woonda, wamfupi, wojintcha; kapena, ife, ife sitikudziwa, kotero inu simungadziwe konse.

⁶⁶ Koma ine ndikunena chimene Iye akanati adzakhale, ngati Iye atakhala pano lero, Iye angadzakhale Mawu a Mulungu. Ichu ndi ndendende chimene Iye anali, ndipo Iye akadali. Iye ndi Mawu, osati Mawu olembedwa okha (Iye ndi Mawu olembedwa), koma chiwonetsero cha Mawu olembedwa. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjantsa dziko kwa Iyemwini.” Mulungu, Mawu, anawonetseredwa mu thupi, ndi cholinga chakuti Mawu Ake adzakhaze kuyankhulidwa kudzera mmilomo ya munthu ndi kukhala Mawu. Ndipo Iye anawonetseredwa mu thupi, ameneyo anali Yesu Khristu, Mulungu, Emanuele.

Tsopano inu mukuti, “Kodi Iye ndi Mawu?”

⁶⁷ Yohane Woyera, mutu wa 1, amatiuza ife, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu.”

⁶⁸ Kodi zina mwa zinthu zimene Iye akanachita zinali zotani? Ife tikupeza kuti, mu Ahebri, mutu wa 4 ndi ndime ya 12, Baibulo linanena kuti, “Mawu a Mulungu ndi akuthwa kuposa lupanga lakuthwa konsekonse, ndipo Iwo ndi ozindikira malingaliro a mu mtima.” Mawuwo ali. Kotero Mawu ndi ozindikira malingaliro ndi zolinga zamu mtima. Izo zikanamuyenereza Yesu, ndendende, kukhala Mawu. Iye ankadziwa malingaliro amene anali mu mtima mwawo. Ahebri 4:12.

⁶⁹ Tsopano ngati ife tikanafuna kuti timuzindikire Iye, kodi ife tikanamuyembekezera Iye kuti akhale Dokotala wina wa

Zauzimu? Palibe umboni wa Iye kuti anayamba wakhalapo konse mu sukulu.

⁷⁰ Kodi ife tingamuzindikire Iye ndi chipembedzo chirichonse? Iye anabwera mu nthawi imene kunali zipembedzo zambiri, koma Iye sanadziyanjanitse Yekha ndi chirichonse cha izo. Kotero Iye...Ife sitikanakhoza kunena kuti Iye anali Mfarisi, kapena Msaduki, kapena ena—ena otero. Ife sitikanatha kumuzindikira Iye ndi chipembedzo chinachake.

⁷¹ Iye anabwerera anthu. Mulungu, pokhala Mulungu wa zonse, Iye ndi Mulungu wa chirengedwe chonse. Iye anafa kuti adzapulumutse ochimwa mu mpingo uliwonse, kuti—kuti adzachiritse munthu wodwala aliyense. Iye anabwera kuti adzawalandire iwo amene akanati adzawalandire Iye.

⁷² Umo ndi momwe Iye aliri pano usikuuno, kuti awachiritse iwo amene ati amulandire Iye, kuti adzawapulumutse iwo amene ati amulandire Iye. Iye amabwera mmawonekedwe omwewo, mwa njira yomweyo.

⁷³ Ngati Iye angabwere, Iye akuyenera kubwera mu kuzindikiritsidwa Mwamalemba. Ngati Iye sanazidzindikiritse Yekha...Palibe malo amene ife tingakhoze kuwapeza mu Baibulo, mu Chipangano Chakale, koma chimene Iye anazidzindikiritse Yekha molondola ndi Lemba, mochuluka kwambiri mwakuti Iye anati, “Ndani, ndi ndani wa inu anganditsutse Ine za tchimo?”

⁷⁴ Tsopano, ife tonse tikudziwa kuti *tchimo* ndi, “kusakhulupirira.” “Iye amene sakhulupirira watsutsidwa kale.” Tsopano, tchimo ndi chotsatira cha kusakhulupirira. Kusuta ndudu si tchimo. Kuba si tchimo. Kunama si tchimo. Kuchita chigololo si tchimo.

“Icho ndi chiyani ndiye?” inu mungatero.

⁷⁵ Ndi zotsatira za kusakhulupirira. Ngati inu mukanakhala wokhulupirira, inu sibwenzi mukuchita zinthu zimenezo. Chifukwa chimene inu mumachitira zimenezo, zimatsimikizira kuti ndinu wosakhulupirira. Mukuona? Pali magawo awiri okha, ndiwo, mwina ndinu wokhulupirira kapena wosakhulupirira.

⁷⁶ Ndipo momwe, nthawizonse zakhala zikundidodometsa ine, kuti munthu akhoza kudzinenera kuti ali ndi Mzimu Woyera mwa iye, ndipo nkumakana Mawu a Mulungu kukhala owona. Pamene, Mzimu Woyera Iwowo unalemba Mawu a Mulungu. Ndipo inu mukudziwa kuti Iye sangadzitche Yekha kukhala wolakwika. Kotero Iye analemba Malemba, ndipo Iye amaimea nawo Malemba, ndipo Mulungu amawayang’anira Iwo, kuti awatsimikizire Iwo.

⁷⁷ Chotero tiyeni tingobwerera mmbuyo ndi kukapeza chimene Iye anali, ngati ife tikufuna kuti tidziwe ngati Iye ali yemweyo lero. Njira yoona yokhayo yopezera, chimene Iye ali lero, ndi kuti

tibwerere mmbuyo ndi kukapeza chimene Iye anali dzulo, ndiye ife tidziwa chimene Iye ati adzakhale lero. Kodi izo ndi zabwino mokwanira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ngati ife tingathe kupeza chimene Iye anali dzulo!

⁷⁸ Ndithudi, ife tikhoza kuyamba kubwerera mmbuyo ndi nkhani yaitali. Ine sindikufuna kuti ndikusungeni inu motalikitsa, chifukwa muyenera kuti mudzakhale pano mawa, ndipo ife tikufuna kuti tikhale ndi mzere wa pemphero, koma ine ndikufuna kuti inu muzitenge izi kwenikweni tsopano ndipo mumvetsere mwatcheru. Ngati tingathe kungobwerera mmbuyo ndi kukapeza chimene Iye anali dzulo, ife tikhoza kupeza ndiye chimene Iye ali lero, chifukwa Baibulo linati, “Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

⁷⁹ Chifukwa chimene ine ndimatembenezira masamba amenewo mmbuyo, chinali chakuti ndipeze kumbuyo kuno kuti... Ine ndinayamba ndipo ndinawerenga Yohane Woyera 12:20, tiyeni tingopitiriza mu Yohane Woyera. Ife tikhoza kuzitenga izo paliponse m’Malemba pamene inu mungafune kutero, chifukwa Bukhu lonseli ndi umboni wa Yesu Khristu. Ndi vumbulutso lathunthu la Yesu Khristu. Palibe chimene chingakhoze kuwonjezedwa kwa Ilo kapena kuchotsedwa kwa Ilo. Icho ndi chimene Iye ali. Iye ndi Emanuele, ndipo izo—izo zikukhazikitsa izo; ziribe kanthu chimene ife tingayesere kumupanga Iye, chinachakenso, kapena mneneri, kapena—kapena chinachake chonga icho. Iye anali mneneri; Iye anali woposa mneneri. Iye ndi mneneri-Mulungu. Koma Iye anali—Iye anali woposa zimenezo. Iye anali Emanuele; osati munthu wabwino chabe, mphunzitsi, wambalume. Iye anali zonsezo, nayenso, ndi kuphatikizirapo chimenecho. Mukuona?

⁸⁰ Tsopano mu Yohane Woyera, ya 1, ife tiyamba usikuuno, ndipo mwinamwake mawa tidzatenga ilo pang’ono, Bukhu lina. Tiyeni tiyambire mu Yohane Woyera 1. Ife tikupeza kuti... Ife tonse tikudziwa kubadwa Kwake kwa namwali, momwe Mulungu anamufungatirira namwali, ndipo analenga khungu la Magazi limene linabala Mwanayo, Khristu Yesu. Ndipo pa gombe la Yorodani, pamene Mulungu anabwera pansu mmawonekedwe a Kuwala, kapena nkunda, palibe aliynse amene anaziwona izo koma Yohane. Anthu onsewo amene anayima pozungulira, sanakuwone Iko. Palibe amene anakuwona Iko koma Yohane. Iye anali yekhayo amene ankakuyembekezera Iko, kotero Mulungu anali atamuza iye kuti akanadzakuwona Iko.

⁸¹ Iwe umangowona chimene ukuchiyembekezera. Ngati mwabwera pano usikuuno mukumuyembekezera Khristu, inu mumuwona Iye. Ngati inu mwabwera kuti mudzatsutse, inu mukhala nazo zochuluka, zochuluka pa dzanja lanu zoti muzitsutse. Zimatengera chimene inu mukuchiyembekezera.

⁸² Yohane anati, “Iye amene anandiuzwa ine mu chipululu kuti ndipite ndikabatize ndi madzi, anati pa iye amene ine ‘ndidzawone Mzimu ukutsika ndi kudzakhallabe, Iye ndi Mmodziyo amene ati adzabatize ndi Mzimu Woyera ndi Moto.’” Yohane anachitira umboni, anati, “Ine ndinawona Mzimu wa Mulungu ukutsika kuchokera Kumwamba, monga nkunda, ndipo Iwo unapita pa Iye.” Ndiyeno Iye anatsogoleredwa kupita ku chipululu, ndi kukayesedwa. Anatuluka mchipululu, ndipo mwamsanga, ife tikumupeza, akupempherera odwala.

⁸³ Tsopano, inu mwaona, chinthu choyambirira, Mzimu wa Mulungu unabwera pa Iye utumiki Wake usanayambe, kotero ndi chifukwa chake Iye amakhoza kunena kuti, “Si Ine amene ndikuchita ntchitozi, ndi Atate amene akukhala mwa Ine. Iwo akuchita ntchitozi.” Tsopano ife tikupeza kuti utumiki Wake unayamba, anayamba kuchiritsa odwala, mwa—mwa pemphero.

⁸⁴ Tsopano Mulungu amachiza mwanjira zambiri. Dokotala anandifunsa ine, osati kale kwambiri, anati, “Lingaliro lanu ndi lotani pa mankhwala, M’bale Branham?”

⁸⁵ Ine ndinati, “Chabwino, Mulungu ndi Mmodzi yekhayo amene angathe kuchiza, bwana.” Ine ndinati, “Baibulo silimanama, ndipo Baibulo linati, ‘Ine ndi Ambuye, ndimachiza nthenda zanu zonse.’” Ndipo ine ndinati, “Baibulo silinganame.” Ine ndinati, “Mulungu amachiza ndi mankhwala. Mulungu amachiza ndi chikondi. Mulungu amachiza ndi kumvetsetsa. Mulungu amachiza ndi chisamaliro. Mulungu amachiza ndi pemphero. Mulungu amachiza ndi zozizwitsa. Chinthu chonsecho, Mulungu amachiza. Ndizo zonse, zonse zomwe ziripo kwa izo, Iye ndi mchiritsi.”

⁸⁶ Ife tiribe mankhwala amene angakhoze kulenga, ndi kulenga khungu mdzanja lanu, kuti achiritse; kulenga mthupi lanu, kuti achiritse. Tikhoza kuzula dzino, tikhoza kudula thumbu, kapena kuchotsa ndulu, koma ndani anachiritsa? Mulungu. Palibe mankhwala amene angamange minyewa, Mulungu yekha. Moyo umamanga minyewa. Mulungu ndiye mchiritsi yekhayo, ndipo ife tinali tikuyankhula pa zimenezo.

⁸⁷ Ndipo ife tikupeza tsopano, kuti Yesu ankapita kumakachiritsa odwala. Ndipo panali mmodzi wa ophunzira Ake dzina lake Andreyana.

⁸⁸ Ndipo ine ndikufuna kuti ndizipange izi mwa sewero chifukwa pali ana akhala pano, ndi mtsikana wamng’ono wodwala wagoni panso pamene. Ine ndikufuna kuti iye azimvetse zimenezi.

⁸⁹ Inu mukudziwa, Andreyana anali mchimwene wake wa Simoni, amene mtsogolo mwake anadzatchedwa Petro. Ndipo Andreyana anali wo—wophunzira wa Yohane. Ndipo Yohane anali atalengeza kuti kunali kukubwera Mesiya, ndipo iye anali wotsimikiza kuti izo zikanadzakhala mu kam’badwo kake.

Ndi chifukwa chake iye sanapite konse ku masukulu aliwonse kapena ku seminare. Ntchito yake inali yofunikira kwambiri.

⁹⁰ Bwanji, inu mukudziwa, ngati wansembe akanamvetsa kuti iye anali woti adzalengeze kubadwa . . . kapena Mesiya wakudza, ndi kudzamudziwitsa Iye kwa dziko lapansi, bwanji, iwo akananena kuti, “Tsopano, tsopano, Dokotala Yohane, kodi inu simukumverera kuti M’bale *Wakuti-ndi-wakuti* ameneyo pano, kodi inu simukuganiza kuti iye ndi woyenera basi kuti akhale Mesiya? Bwanji, tayang’anani pa iye, iye—iye—iye ali ndi mbiri yabwino. Inu mukudziwa inu mukudziwa zimenezo, ameneyo ndi Mesiya. Bwanji inu simukupita ndi kukaliwuza dziko?”

⁹¹ Koma, mwaona, ntchito yake inali yofunikira kwambiri kuti ikopedwe ndi munthu. Iye anapita mchipululu ndipo anakayembekezera mu seminare ya kuphunzitsa kwa Mulungu, kufikira Mulungu atamuuya iye kuti, “Pa Yemwe iwe uti udzawone Mzimu ukutsika, ameneyo ndi Mmodziyo woti adzamulengeze, Mesiya.” Mukuona?

⁹² Tsopano ife tikupeza kuti Andreyana anakhulupirira zimenezo, sindikukaikira anabwerera ndipo anakamuuya Simoni za izo, nthawi zambiri. Koma Simoni, pokhala ngati wouma mutu pang’ono, monga ife . . . Mundikhululukire kafotokozedweko; ine ndikuyembekeza kuti izo sizikumveka mosinjirira. Koma iye, pokhala ngati wouma mutu pang’ono, monga ife tingazitchulire izo lero, “Oh, pitirira, ngati iwe ukufuna kumvetsera kwa izo.” Ndipo tsiku lina iye anabwera ndipo anadzamuuya iye kuti iye anali atamupeza Mesiya, ndipo iye analephera kuti azikhulupirire zimenezo.

⁹³ Ndipo ine ndikutha kumuwona Andreyana akumubweretsa Simoni tsopano pamaso pa Ambuye Yesu. Nthawi yoyamba imene iye anamuwonapo Iye. Yesu anali atangobwerera kuchokera ku chipululu. Utumiki Wake unali ukuyamba, tsopano Iye ankayenera kuti azindikiritsidwe. Ndipo mwamsanga pamene Simoni anayenda kufika mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, Yesu anayang’ana pa iye ndipo anati, “Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa Yona.”

⁹⁴ Tsopano nthawiyomweyo ife tikupeza kuti Simoni anakhulupirira. Iye ndiye anapatsidwa dzina la Petro. Nchifukwa chiyani iye anakhulupirira zimenezo?

⁹⁵ Ine ndinawerengapo nkhani ya abambo ake, a Yonasi, anali munthu wopambana wa—wa pemphero. Iye anali atawalera anyamata ake kuti—kuti azikhulupirira mwa Mulungu. Ndipo tsiku lililonse ntchito yawo inali kuwedza, nthawi zambiri ankayenera kugwada pa mawondo awo ndi kupemphera kuti Mulungu awapatse iwo nsomba zambiri koteru iwo amakhoza kulipira ngongole zawo ndi kupeza mkate wa tsiku limenelo.

⁹⁶ Ndipo iye asanafe, munthu wachikulireyo anakhala pa mphepete pa ngalawa yake tsiku lina, ndipo iye anati

kwa anyamatawo, iye anati, “Ana, ife ndi Ahebri, ndipo ife timakhulupirira kuti kuli Mesiya amene akubwera. Ndipo ine nthawizonse ndakhala ndikuyembekezera kuti ine ndidzakhala moyo kuti ndidzawone tsiku limene ndidzawuwone Mesiya akupondetsa mapazi Ake pa dziko lapansi. Ndipo ine...koma ine ndikuganiza kuti sindikhala moyo kufikira nthawi imeneyo, chifukwa ndakalamba tsopano ndipo ine ndikuyenera kuti ndizipita. Koma, anyamata, Satana sadzalola kuti Mesiya ameneyo adzawuke popanda amesiya ambiri onyenga poyamba. Kotero ine ndikufuna kuti anyamata inu muzikumbukira, musadzadabwitsidwe ndi—zinthu zambiri zomwe ziti zidzachitike. Koma ine ndikufuna kuti anyamata inu mulangizidwe. Kumbukirani, kuti ife tiri ndi ichi: Mesiya, pamene Iye adzabwera, Iye adzayenera kuti adzazindikiritsidwe Mwamalemba ndi Mulungu, Iye asanakhale Mesiya.” Ife tikusowa azibambo ochulukira monga amenewo lero!

⁹⁷ “Iye adzayenera kukhala Mesiya Mwamalemba. Ndipo tsopano ife tamutsatira Mose, mneneri wankulu amene anawatsogolera anthu athu kutuluka mu Igupto, ndipo ife tamvetsera ku kuphunzitsa kwake. Ndipo ife—ife tikudziwa kuti—kuti Mose ankalandola. Ndipo mu Deuteronomi, mutu wa 18, Mose anatiuza ife kuti, ‘Mesiya; Ambuye Mulungu wanu adzawutsa mneneri wonga ine, ndipo iwo akuyenera kudzamumvera Iye.’”

⁹⁸ Tsopano, Israeli nthawizonse ankaphunzitsidwa kuti azingokhulupirira aneneri. Inu aphunzitsi a Baibulo mukudziwa zimenezo. Ndipo mneneri ankakhoza kokha kuzindikiritsidwa, kukhala mneneri, pamene iye anenera ndipo chinthu chimene iye waneneracho chikafika podzachitika. Baibulo linati, “Ngati pakhala mmodzi pakati panu, amene ali wauzimu kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzayankhula kwa iye, ndi kudzizindikiritisa Ndekha kwa iye, mmasomphenya ndi mmaloto. Ndipo chimene iye anena chikafika podzachitika, ndiye mumumvere iye. Koma ngati icho sichichitika, musamuwope iye.” Chimodzimodzi, ndicho chimene Iye anamuuza Mose kuti awauze anthu, ndipo chimenecho chinali chizindikiritso chawo cha Lemba kuti Mesiya akanadzakhala mneneri.

⁹⁹ Tsopano aliyense akudziwa kuti Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri; osati kwa wansembe, koma kwa mneneri. Baibulo linanena chomwecho. Mawu a Ambuye amadza kwa mneneri. Ndipo ife tikudziwa, ngati iwo ali Mawu a Ambuye, ndipo mneneriyo ndi woona, ndiye mawu akewo ndi owona, zikatero mawu ake amafika podzachitika. Ndipo ndizo ziyenerezo zake, kuti, poyamba, ndi Mawu. Ndipo, choyamba, Mulungu ndi Mawu. Ndiyeno ngati iye ayankhula mawu, ndipo izo nkuchitika, ndiye izo zimawonetsera kuti Mulungu wamukhazitsa Mwauzimu munthu ameneyo.

¹⁰⁰ Tsopano ndiye ndi zimenezo mmalingaliro, iwo akhoza kukhala kuti anawutsa mitundu yonse ya zogirigisha ndi china chirichonse mdziko, ophunzira Baibulo amenewo sakanakhulupirira zimenezo, chifukwa Mesiya ankayenera kukhala mneneri. Ndipo iwo anali asanakhale ndi mneneri kwa zaka foro handiredi. Malaki anali mneneri wotsiriza. Kunalibe mneneri.

¹⁰¹ Ndipo apa pakubwera Simoni, ndi kuphunzitsa koteroko monga kumeneko, kufika mu kukhalapo kwa Munthu yemwe m'bale wake molimba ankakhulupirira kuti Iye anali Mesiya. Ndipo mwamsanga pamene iye anayenda kudzafika mu Kukhalapo Kwake, osati kokha kuti Iye ankadziwa yemwe iye anali, Iye ankamudziwa bambo wokalamba waumulungu uja, Yonasi. Nzosadabwitsa kuti izo zinachotsa kukhuthalako mwa iye. Iye anadziwa kuti icho chinali chizindikiritso choona cha Mesiya. "Lako, dzina lako ndi Simoni, ndiwe mwana wa Yonasi."

¹⁰² Ndipo munthu amene anali wosaphunzira kwambiri mwakuti iye sankakhoza ngakhale kulemba dzina lake lomwe, ife timauzidwa; Baibulo linanena, mu Bukhu la Machitidwe a atumwi, mutu wa 3, kuti, "iye anali ziwiri zonse mbuli ndi wosaphunzira." Koma chinamukomera Mulungu kumupanga iye kukhala mutu wa mpingo ku Yerusalemu, ndi kumupatsa iye makiyi aku Ufumu. Chifukwa, pamene mbewu yokonzedweratu ija inali mmenemo mwa nsodzi wachikulire uja, ndipo pamene Kuwala kunadzaikhudza iyo, mwamsanga iyo inazindikira kuti ameneyo anali Mesiya.

¹⁰³ Tsopano zimenezo zinatsimikizira pamenepo, kuti munthu ameneyo ankadziwa, izo zinatsimikizira kuti mbewu imeneyo inali itagona mmenemo. Dzina lake linali pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa chikhazikitsireni maziko a dziko lapansi, pamene Mwanawankhosa anaphedwa mu kuganiza Komwe kwa Mulungu. Ndipo mwamsanga pamene Kuwala kunadzaikhudza iyo, mwamsanga iyo inabwera ku moyo ndipo inazindikira kuti iye anali Mesiya.

¹⁰⁴ Panali wina atayima pamenepo dzina lake Filipino, ndipo iye anawona izi, mwamsanga zinabwera mmalingaliro ake. "Zoonadi ndi Iyeyu, pakuti ine ndikuwadziwa Malemba. Munthu Ameneyo anali asanamuwonapo konse munthu ameneyo, ndipo Iye akanadziwa bwanji yemwe iye anali? Ameneyo ndi Mneneri."

¹⁰⁵ Ananyamuka kupita kwa mzake amene ankachita naye maphunziro a Baibulo, kuyambira ali mnyamata. Dzina lake anali Nataniele. Ndi mamailosi fifitini kuchokera kumene iwo ankalalikira, kuzungulira phiri, kupita kumene Nataniele anali ndi mitengo ya azitona. Ine ndikukhoza kumulingalira Filipino

ali pa ulendo wake, akulumpha ndi kufuula. Iye anali atapeza chinachake chimene chinali chenicheni.

¹⁰⁶ Oh, momwe Izo zikuyenera kuyambitsira mitima yathu, kuzungulira mapiri, kudutsa mmadambo, kutsika kudutsa mminda, kutsika mkanjira, kuwoloka msewu, kudutsa fuko, kwinakwake.

¹⁰⁷ Iye anakapeza chinachake. Ndipo iye anali ndi mzake. Kuphuzira kwa Baibulo, kwammbuyo, kunali kutatsimikizira kuti Mesiya wa Mwamalemba uyu akanadzakhala Mneneri. Kunali kulibe aneneri kwa zaka foro handirede.

¹⁰⁸ Pamene iye anabwera pa malopo, iye anamupeza Nataniele kunja pansu pa mtengo, akupemphera. Ndipo mwinamwake iye anayima kwa mphindi pang'ono chabe, kuti adikirire, monga njonda ya Chikristu, kudikirira mpaka iye atatsiriza pemphero lake. Ndipo pamene iye anadzuka, mwinamwake anali akusasa fumbi pa mkanjo wake, Filipino mwamsanga akhoza kukhala kuti anati, "Nataniele!"

Ndipo iye anabwera pamenepo, anati, "Filipo, mzanga, ndine wokondwa kukuwona iwe!"

¹⁰⁹ Ndipo mwinamwake kukambiranako kunali chinachake monga chonchi. Mwaona, iye analibe nthawi yoti anene kuti, "Kodi mitengo ya azitona ikuchita bwanji?" Kapena, "Kodi mkazi ndi mwana ali bwanji?" Mwaona, uthengawo unali wachangu. Iye anali atawona chinachake. Iye anali atawona Mesiya wozindikiritsidwa, ndi Lemba, ndipo chimenecho chinali chimene iwo anakhala akuchiyembekezera kwa zaka ndi zaka ndi zaka. Iye anati, "Bwera, udzawone Amene ife tamupeza! Yesu waku Nazareti, mwana wa Yosefe, bwera, udzamuwone Iye!" Uthengawo unali wachangu.

¹¹⁰ Ine ndikukuuzani inu, abale, ngati ife tikanangokhala ndi kutengeka kwa mtundu umenewo, kuti Uthenga wathu ndi wachangu kwambiri. Ife tiribe nthawi ya zopusa. Tiyeni tiwutengere Uthengawo kwa anthu, anthu amene awukhetsera thukuta iwo kupyolera mu kuzunzidwa, ndiwo ana a makolo athu amene ankayima mmisewu, ali ndi—ali ndi nkhotcho mdzanja lawo, ndipo anakhoza kumadya chimanga pa njanji, kuti akathandizire Msewuwaukulu uwu, Uthenga uwu. Ndipo tsopano onani Khristu pakati pathu, tiyeni tiwufikitse Iwo ku dziko lapansi, mwamsanga momwe ife tingathere, ndi kukamupeza iye.

Anati, "Bwera, udzawone Amene ife tamupeza."

¹¹¹ Tsopano ife tikupeza kuti Nataniele anali wazafioleje ndithu, ndipo ine ndikukhoza kulingalira iye akunena kwa Filipino, "Tsopano dikira miniti chabe, Filipino, kodi iwe wachita misala ya mtundu wanji?" Inu mukudziwa, kuyankhula kumeneko kukuyendayendabe lero, mwaona. "Kodi iwe wasokonezeka mwamtundu wanji?" Kusokonekera

kwinakwake, inu mukudziwa. “Ine—ine ndikukudziwa iwe ngati munthu wabwino, woganiza bwino, ndipo apa iwe ukubwera ukuthamanga ndi kudzandiuza ine kuti Mesiya ali pano pa dziko lapansi?”

¹¹² Iye ayenera kuti anayankhule ndi m’magi. Inu mukudziwa, amagi amakhala uko ku Babeloni. Iwo anali Ayuda kumtunda uko akuphunzira zammwamba. Ndipo pamene iwo anawona nyenyezi zitatu zimenezo zikubwera mu mzere, icho chinali chizindikiro, chizindikiro chakale cha Chihebri, kuti pamene nyenyezi zitatu zinabwera mu mzere, Mesiya anali pa dziko lapansi. Iwo anabwera, akufuula, “Alikuti Iye, wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? Ife tinaiwona Nyenyezi Yake ndipo ife tabwera kuti tidzamupembedze Iye.”

¹¹³ Koma, Filipino, uyu...Iwo analibe njira zofalitsira mauthenga zosiyanasiyana monga televizioni, wayilesi ndi nyuzipepala, ndi zinthu mmasiku amenewo, ndipo iwo sakanatha kufalitsa chirichonse chonga icho mulimonse. Kotero chinthu choyamba ife tikudziwa, ife tikumupeza Filipino ndi Nataniele akuyankhula, “Chabwino,” iye anati, “bwera.”

¹¹⁴ Iye anati, “Taona, kodi chinthu chabwino chirichonse chingachokere mu gulu la oyera-...” kapena mundikhululukire ine, “gulu la anthu monga amenewo, kuchokera ku Nazareti?”

¹¹⁵ Chabwino, inu mukudziwa chimene ine ndikuganiza? Filipino anamupatsa iye yankho labwino kwambiri limene aliyense akanakhoza kumupatsa munthu. Iye sanayesere kuti afotokoze zimenezo. Iye sanayesere kuti apite mu tsatanetsatane wa zimenezo. Iye anangoti, “Bwera ndipo udzawone. Bwera, udzadziwonere wekha. Ika mpukutu umenewo pansu pa nkono wako, wa Deuterome 18, ndipo bwera unditsatire ine ndipo ife tikapeza.”

¹¹⁶ Tiyeni titenge zokambirana zawo pamene iwo ankayenda. Mwaona, iwo ankayenera kuti akafike kumeneko, tsiku limodzi, ndi kubwereranso tsiku lotsatira, mamailosi fifitini. Kotero ali panjira, akuzungulira, ndikutha kumumva Filipino akunena kuti, “Tsopano taona, Nataniele, maphunziro a Baibulo ochuluka monga ife tinali nawo aja, ife tikukhulupirira mokhazikika kuti Mesiya ali woti adzakhale Mneneri-Mulungu, chifukwa Mose ananena chomwecho. Ndipo ife takhala tikumutsatira Mose, ndipo timayenera kuti tizimutsatira iye mpaka Mneneri uyu atadzafika. Ndipo pamene Mneneri uyu adzabwera powonekera, ndiye Iye adzatiuza ife njira ya moyo, kuyambira pamenepo mpakana mtsogolo. Ndipo ngati...Inu mukudziwa, amene sadzamukhulupirira Iye adzadulidwa kuchokera pakati pa anthu, ngati ife sitidzamukhulupirira Iye.”

“Chabwino, iwe ukudziwa bwanji kuti munthu uyu ndi Mneneri?”

117 Anati, “Kodi iwe ukumukumbukira nsodzi wachikulire uja kumusi uko, yemwe iwe unamugula nsomba za tsiku limenelo, ndipo iye analibe maphunziro okwanira kuti alembe dzina lake pa lisiti?”

“Eya, ine ndikumukumbukira iye. Oh, dzina lake linali Simoni. Inde.”

118 “Mchimwene wake, Andrey, wakhala akupita ku misonkhano ya Yohane. Ndipo pamene iye anawona kulengezako, ndipo anamva kulengeza kwa Yohane, akuti, ‘Uyu anali Mesiya.’ Ndipo, Yohane, ife tikudziwa kuti anali mneneri, kotero iye sakanakhoza kunena kanthu kolakwika. Iye analengeza kuti, ‘Ameneyo ndi Mesiya,’ ndipo kotero iye anati anawona chizindikiro pa Iye. Ndipo iye anamubweretsa mchimwene wake dzulo. Ndipo mwamsanga pamene iye anayenda kupita mu Kukhalapo Kwake, Iye anati, ‘Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa a Yonasi.’ Bwanji, izo sizingandidabwitse ine ngati Iye sangandiuze ine yemwe iwe uli, pamene iwe ukafike kumeneko,” iye angakanene.

119 “Oh,” iye anati, “tsopano dikirani miniti, dikirani miniti! Ine ndikuyenera kukadziwonera ndekha zimenezo. Ine—ine—ine ndikuyenera kukaziwona zimenezo.”

120 Kotero ife tikupeza apa, tsiku lotsatira, chimene chikuchitika. Iwo anafika, magulu aakulu a anthu anali atayima. Yesu mwinamwake anali akuyankhula. Mwinamwake iwo anali atakhala, ambiri a iwo, mwinamwake iwo anali ataimirira; ine sindikudziwa. Koma, komabe, Filipino anabwera, ndipo iye anamubweretsa Nataniele pamenepo, ndipo pamene Yesu anatembenuka ndi kuyang’ana pa iye, Iye anati, “Taonani m’Israeli, m’Israeli ndithudi, amene mwa iye mulibemo chinyengo.”

121 Bwanji, izo zinamudodometsa munthu ameneyo! Iye anati, “Rabbi, motani, Inu munadziwa bwanji chirichonse cha ine? Ine—ine—ine—ine sindikukudziwani Inu. Ndipo Inu simunandiwonepo ine, ndipo ine sindinayambe ndakuwonanipo Inu. Motani, Inu mungadziwe bwanji chirichonse chokhudza ine?”

122 Iye anati, “Chabwino, Filipino asanakuyitane iwe, iwe unali pansu pa mtengo. Ine ndinakuwona iwe.” Oh, mai, maso amtundu wanji! Dzulo lake, ndipo mailosi fifitini kuzungulira phirilo, “Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.”

123 Kodi wophunzira uyu, mwana wa Mulungu, woti akhale, kodi iye anaphunzira chiyani? Iye anaphunzira kuti icho chinali chizindikiritso cha Mesiya. Kodi iye anachita chiyani? Sindikukaikira iye anayang’ana pozungulira ndipo anamuwona wansembe wake, ndi ena onse a iwo, ataimirira. Iye anathamangira ku mapazi Ake, ndipo anakagwera pansu, ndipo

anati, “Rabbi, Inu ndi Mwana wa Mulungu. Inu ndi Mfumu ya Israeli.”

¹²⁴ Yesu anati, “Iwe wakhulupirira chifukwa ine ndakuuza zinthu izi. Tsopano iwe uwona zazikulu kuposa izi.”

¹²⁵ Oh, koma pamnepo panali ena amene anayima pambalipo, ansembe, abusa. Ndipo iwo ankadziwa kuti ankayenera kukayankhira kwa osonkhana awo, chifukwa cha zimenezo, kotero iwo ankayenera kuti anene chinachake. Inu mukudziwa chimene iwo ananena? “Munthu uyu ndi Bezezebule. Iye ndi wam’bwebwe chabe, kapena mtundu wina wa mdierekezi.”

¹²⁶ Ndipo Yesu anatembenuka ndipo anati, “Inu mukayankhula zimenezo momutsutsa Mwana wa munthu, izo zidzakhululukidwa kwa inu. Koma pamene Mzimu Woyera udzabwera mukadzachita chinthu chomwecho; kuti mudzayankhule mawu amodzi mowutsutsa Iwo, sizidzakhululukidwa konse mdziko lino ngakhale—ngakhalenso mdziko limene liri nkudza.” Ndi malo otani amene izo zikanatiyika ife pamenepo!

¹²⁷ Tsopano ife tikupeza kuti, kudutsa mpaka mmusi, ife tikanakhoza kupita kudutsa m’Malemba. Iwo. . .Tiyeni titenge tsamba lina ndi kutsegula Baibulo kachiwiri. “Ife tinkasowa kuti tipite ku Samariya,” tsiku lina pamene Iye anali pa ulendo Wake waku Yeriko. Yeriko anali mmusi mwa phiri, ndipo Yerusalemu anali pa phiri. Samariya ndi komwe kumbuyo, zikanakhala ngati kupita ku—kupita ku California kudzera ku—ku Hot . . . kudzera ku Little Rock. Inu mukanalambalala mozungulira. Koma Iye ankayenera kuti apite ku Samariya. Tsopano ife tikupeza kuti, Asamariya, iwo anachokera ku—gulu losakanikirana la anthu.

¹²⁸ Pali mitundu itatu yokha ya anthu pa dziko lapansi, ndiyo: Anthu a Hamu, a Shemu, ndi a Yafeti. Ngati ife timalikhulupirira Baibulo, iwo onse anayambira kuchokera kwa ana a Nowa, ndipo icho ndi chimene chinatuluka kuchokera mdziko.

¹²⁹ Ndipo tsopano ife tikupeza zimenezo: Myuda, ndi Wamitundu, ndi Msamariya. Petro, ali ndi makiyi operekedwa kwa iye pa Pentekoste, iye anatsegula izo pa Pentekoste, kwa Ayuda, iye anatsegula izo kwa Asamariya, ndipo anatsegula izo kwa Amitundu. Kenako mtundu wonse, mitundu yonse, inali itamva Uthenga. Simukumumvanso iye akugwiritsa ntchito makiyi, chifukwa Uthenga unali utatsegulidwa kwa onse a iwo. Zindikirani tsopano.

¹³⁰ Asamariya awa anali theka Myuda ndi Wamitundu. Iwo ankakhulupirira mwa Mulungu yemweyo amene Myuda ankamukhulupirira, ndipo iwo ankayembekezera kubwera kwa Mesiya.

¹³¹ Tsopano, Mesiya adzangowonekera kokha kwa iwo amene akumuyembekezera Iye. Mukuona? Tsopano ife Amitundu

sitinkayembekezera Mesiya aliyense, ndipo ife sitinayambe tamuwonapo aliyense. Ili ndi tsiku lathu.

¹³² Kotero a—Asamaria an kayembekezera Mesiya. Ndipo ngati Mesiya anali pa dziko lapansi, zinali zokakamizika, kwa anthu Achisamariya, kuti adzizindikiritse Yekha monga Iye anachitira kwa Ayuda.

¹³³ Tsopano aliyense wa ife akudziwa kuti Mesiya anadzizindikiritse Yekha pokhala mneneri amene Mose ananena kuti Mulungu akanadzamuukitsa. Ndi angati akukhulupirira zimenezo, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndithudi.

¹³⁴ Iye anali Mneneri. Iye anazindikiritse. Tsopano, ameneyo anali Yesu dzulo. Ndipo ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, uyo akhala Yesu lero, chinthu chomwecho.

¹³⁵ Tsopano ife tikumupeza Iye akupita ku mzinda uwu wa Sukari, ndipo—ndipo apo panali cha pafupifupi pakati pa tsiku. Ndipo ophunzirawo anapita kutali mu mzindawo, kuti akagule zakudya zina. Zitumbuwa, izo zimatchedwa chomwecho mu Lemba. Ndipo pamene iwo anali atapita, Yesu anadikirira.

¹³⁶ Ngati inu munayamba mwakhalapo kumeneko, pamakhala powonekera monga chonchi; chitsime, kapena chitsime cha mzinda, chagulu, kunja kwa mzinda. Icho chidakalipobe mpaka lero. Ndipo anthu amatuluka ndi kudzatunga madzi awo, ndi kubwereranso mu mzinda. Ndipo iwo amanyamula iwo pamitu pawo, mitsuko. Ndipo akazi amakhoza kuyika pafupifupi mtsuko wa magaloni faivi pamitu pawo, ndi kuyika umodzi pa ntchafu iliyonse ndi kumayenda, kumayankhula ndi akazi amzawo monga momwe akazi amachitira, ndipo—ndipo osataya ngakhale dontho lamadzi. Ine—ine sindimamvetsa momwe iwo amachitira zimenezo, koma iwo—iwo amachita izo, manyamulidwe angwiro chotero, kumayankhula ndi kumayankhulana monga momwe madona amachitira pamene iwo akuyenda, ali ndi mitsuko iyi, pafupifupi magaloni fifitini a madzi, akumayenda motsatira monga choncho, akuyankhulana. Ndipo akazi awa, chifukwa...Iwo amachitabe chinthu chomwecho basi monga iwo ankachitira nthawi imeneyo, ndipo akazi awa amabwera ku chitsime kuti adzatunge madzi awo.

¹³⁷ Tsopano uko kunali, cha pafupifupi leveni koloko kapena thwelovu, kunali mkazi wa mbiri yoyipa, mukukhala ngati inu mukudziwa chimene ine ndikutanthauza, a—mkazi wa getsi lofiira anatulukira pa chitsimepo kuti adzatunge madzi, ndipo iye anayamba kutsitsa a—mitsuko wa madziwo. Iwo amakhala ndi—chotungira, ndi zingwe ziwiri zimene zimamangirizidwa pa chotungira ichi, kapena chidebe, ndipo iwo amachitsitsira icho mu chitsime, ndipo icho chimatembenukira mmbali pamene icho chigunda madzi, ndipo iwo amawakokera madzi awa

mmwamba. Ndipo iye anali akungokonzekera kuti atsitsire a—chotungiracho pansu, pamene iye anamumva winawake, akuti, “Ndibweretsere Ine akumwa.” Ndipo iye anayang’ana, ndipo anawona a—Myuda atakhala motsamira khoma, pamene mpesa unatsamira pakhoma, ndipo Iye anali atakhala pamenepo. Iye—Iye akuyenera kuti anali ngati Munthu wa usinkhu wapakati, kapena ankawoneka wa usinkhu-wapakati.

¹³⁸ Ine ndikuganiza kuti Iye ankawoneka mokulirapo pang’ono kuposa chimene Iye anali kwenikweni. Chifukwa, ife tikupeza mu Yohane Woyera 6, kuti kukambiranako kunabwera pankhani yakumwa madzi pa . . . mchipululu, ndi zina zotero, ndi—ndi momwe iwo ankasangalalisa ndi mkate, kuimira manna. Ndipo Yesu anati, “Ndine Thantheve lija limene linali mchipululu.”

¹³⁹ Ndipo iwo anati, “Ndiwe Munthu wosapitirira zaka fifite,” mwaona, ndipo Iye anali ndi sarte zokha. “Ndiwe Munthu wosapitirira zaka fifite.” Kupsyinjika Kwake kwakukulu kukuyenera kuti kunaperepesa gawo Lake la umunthu, ndipo Iye akhoza kukhala kuti anali atayamba imvi pang’ono, kapena chinachake. Anati, “Ndiwe Munthu wosapitirira zaka fifite, ndipo ukuti Iwe ‘unamuwona Abrahamu’? Tsopano ife tikudziwa kuti Ndiwe wamisala, kapena wopenga.”

¹⁴⁰ Ndipo Iye anati, “Abrahamu asanakhalepo, INE NDINE.” Iwo ankanang’ana pa munthuyo. Icho chinali chimene chinali mmenemo chikuyankhula. Ndipo “INE NDINE” anali mchipululu ndi Mose, mu chitsamba chonyeka.

¹⁴¹ Ndipo pamenepo ife tikupeza kuti Iye ankawoneka wa usinkhu waung’ono. Ndipo, Iye, iye anamuwona Myuda wa usinkhu wapakati uyu atakhala pamenepo, mwinamwake mwamuna wopitirira usinkhu umene akanati azisewera ndi mkazi woteroyu, ndipo iye anati, “Si chamwambo, Inu pokhala Myuda, kuti mundifunse ine, mkazi waku Samariya, kuti ndikuthandizeni. Ife sitimayanjana.” Mwa kuyankhula kwina, “Ife tiri ndi tsankho kuno, ndipo ife sititero . . . ife sitimayanjana.”

¹⁴² Mwamsanga Iye anamudziwitsa iye. Tsopano Iye anati, anayankhula ndi iye. Ndipo iye anati, “Tsopano inu Ayuda mumati mumapembedza mu Yerusalemu, ndipo, kapena ife timapembedza mu phiri ili,” ndi zina zotero, ndi za momwe chitsimecho chinaliri chakuya, ndipo Iye analibe kanthu koti atungire.

¹⁴³ Ndipo, kukambiranako, tsopano inu mukuyenera kutenga mawu anga apa kwa ichi, chimene Iye anali kuchita, mwaona.

¹⁴⁴ Atate, mu Yohane Woyera 5:19, Yesu anati, “Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita.” Tsopano molingana ndi Mawu Ake Omwe, ndipo Iye sanganame, ndi kukhala Mulungu, molingana ndi Mawu Ake Omwe,

Iye sanachite konse chozizwitsa chimodzi mpaka Mulungu atamuwonetsera Iye mu masomphenya, choti achite, “Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Mwana sangachite kanthu mwa Iyeyekha, koma chimene Iye awawona Atate akuchita, chimenecho amachita Mwanayo chimodzimodzi. Mwaona, Atate amagwira ntchito, ndipo Ine ndimagwira ntchito mowatsatira.”

¹⁴⁵ Tsopano, Atate anali atamuuzza Iye kuti apite njira yaku Samariya, ndipo pamenepo Iye anali atakhala pamenepo, ndiyeno mkazi uyu anatulukira. Tsopano, Iye ankayenera kuti akhudze mzimu wake, kotero Iye ankayenera kuti ayambe kuyankhulana ndi iye. Mukuona? Ndipo Iye anati, Iye atatha kupeza limene vuto lake linali, ife tonse tikudziwa limene ilo linali, Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

¹⁴⁶ Ndipo iye anati, “Ine ndiribe mwamuna.” Oh, ndi chidzudzulo chotani kwa Iye. Mukuona? “Ine ndiri...” Komabe, iye sankadziwa. Iye anali munthu wamba chabe. Iye sanavale monga wansembe kapena rabbi. Iye anali munthu wamba. Mukuona?

Ndipo anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako ndipo mubwere kuno.”

Iye anati, “Ine, ine ndiribe mwamuna aliyense.”

¹⁴⁷ Iye anati, “Iwe wanena zoon. Pakuti wakhala nawo faivi, ndipo amene ukukhala naye tsopano si wako; pa icho iwe wanena zoon.”

¹⁴⁸ Tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire kusiyana kwake pakati pa mkazi ameneyo ndi ansembe ophunzira amenewo amene anamutcha Iye “Belezebule.” Mwamsanga pamene iye anawona zimenezo, iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndi Mneneri. Tsopano, ife Asamariya, ife timawadziwa Malemba. Iye timadziwa kuti pamene Mesiya adzabwera, amene akutchedwa ‘Khristu,’ Iye azidzachita zimenezi. Iye adzatiuza ife zinthu izi. Mwaona, icho ndi chizindikiro cha Mesiya. Chotero Inu mukuyenera kukhala mneneri Wake, chifukwa Iye adzakhala mneneri pamene Iye adzabwera. Iye sitinakhale naye mmodzi kwa mahandirede a zaka. Koma pamene Iye adzabwera, ife tikudziwa kuti Mesiya azidzachita zimenezi.”

Yesu anati, “Ine ndine Iye, amene ndikuyankhula ndi iwe.”

¹⁴⁹ Ngati chimenecho chinali chizindikiro cha Mesiya dzulo, icho ndi chizindikiro cha Mesiya lero, chifukwa Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Icho sichinali chizindikiro kwa afioroje. Icho chinali chizindikiro kwa okhulupirira.

¹⁵⁰ Mkazi ameneyo ankadziwa zochulukira za Malemba kuposa momwe ansembe aja ankachitira. Ine ndinena chinthu chimodzi, iye ankadziwa zochulukira za Iye kuposa alaliki ambiri lero. Uko nkulondola. Inde, bwana. Eya, iye anamudziwa Iye. Bwanji? Ine

ndikukhulupirira kuti mbewu ya Moyo Wamuyaya inali mkati mwa mkaziyo. Ndipo pamene Kuwala kuja kunawalira pa Iyo, mwamsanga iye anakuzindikira Iko.

¹⁵¹ Tsopano tayang'anani pa ansembe awo amene akanayenera kudziwa bwinoko. Iwo anati, "Munthu uyu ndi Bezezebule. Iye akuchita izi, Iye ali. . ."

¹⁵² Ndipo Yesu anawauza iwo, "Kuwutcha Mzimu wa Mulungu 'mzimu wodetsedwa,' sizikanakhulukidwa konse." Uwo unali Mzimu wa Mulungu ukuchita zimenezo. "Ntchito za Mulungu, 'mzimu wosayera.'" Ndipo ansembe amenewo, mmalo mofufuza Malemba! Iye anati, "Ngati inu mukanalidziwa tsiku Langa."

¹⁵³ Ngati ife tikanangodziwa kokha tsiku limene ife tikukhalamo, sipakanakhala chisokonezo chochuluka kwambiri chokhudza Uthenga uwu ndi chokhudza Malemba omwe ife tikuyesetsa kuti tiwabweretse kwa anthu, ngati anthu akanangomvetsa kuti ife tiri pa nthawi yotsiriza.

¹⁵⁴ Tsopano, koma, pamene Kuwala kuja kunakhudza mkazi wamng'ono uja, mchikhalidwe chimenecho, dzina loipa, a— a—mkazi wachiwerewere; ndipo ngati Lemba limenelo, ngati Mawu amenewo, Mawu ozindikiritsidwa amenewo. . . Iye anali atawerenga Malemba ndipo iye anakadziwa chimene Mawu ankanena. Ndipo pamene iye anawawona Mawu amenewo akuwonetseredwa, mwamsanga iye anawazindikira Iwo kuti anali Mesiya.

¹⁵⁵ Ngati iye anachita zimenezo pansu pa zikhalidwe zimenezo, kodi ife tingayenere kuchita chiyani usikuuno ngati ife tingamuwone Iye akuchita chinthu chomwecho, Mpingo wobadwa mwatsopano wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ukuyembekezera Kudza Kwake? Izo zikuyenera kukhuthula chikuku chirichonse kudutsa apa. Mai, wochimwa aliyense akuyenera kuti agwere mozungulira guwa. Izo zitsimikizira kuti Iye ali moyo.

¹⁵⁶ Zindikirani, mwamsanga iye anathamangira mu mzinda, ndipo anati kwa mwamunayo, "Bwerani, mudzamuwone Munthu yemwe wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita." Tsopano mwinamwake kukambirana kwake kunali monga chonchi, "Amuna ndi abale, ndiloleni ine ndiyankhule momasuka kwa inu. Kodi uyu si Mesiya amene?" Iye anati, "Bwerani, mudzamuwone Mwamuna Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya?"

¹⁵⁷ Ndipo Yesu anabwera mu mzindamo. Ndipo Baibulo linanena kuti amuna a mzinda umenewo anakhulupirira pa Iye chifukwa cha umboni wa mkaziyo. Iye sanachitenso Izo nthawi ina. Iye sananene chinthu chimodzi chinanso cha Izo. Izo zinakhazikitsa zimenezo. Iye anali Mawu otsimikiziridwa a Mulungu. Iye anali. Iye ndi Mulungu, Mesiya. Tsopano, kwa fuko la anthu monga limenelo! Mukuona?

158 Tsopano ine sindikudziwa basi kuti tiri ndi nthawi yochulukwa bwanji. Ife tiyima mwina mwake basi... Chabwino, dikirani miniti yokha. Yesu anati, mu Luka Woyera, Iye anati, “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Inu mukukumbukira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Tsopano tiyeni tingoyima kwa Lemba limodzi lina, tingofufuza izi motsika.

159 Tsopano, penyani, Iye anadzizindikiritse Yekha. Tsopano, ife tiri nawo malo ambiri. Ife tikhoza kumutenga Bartumeyo wakhungu, ndi kudutsa monse, ndi kuwonetsera mkaziyo akukhudza chovala Chake, zinthu zonsezo kudutsa mu Lemba, ndi pa chitsime pamene Iye analowa mmenemo, ndi kumudziwa mwamunayo pamenepo pa chipata chotchchedwa Chokongola, anali ali ndi vuto ili kwa zaka zambiri, ndi zina zotero, ndipo Yesu ankadziwa. Ndiyeno anapitirira, ndi zina zotero, kudutsa mu Lemba, kupita njira yonse kuyambira ku Genesis. Koma, kuti ndikudziwitseni inu, kuti ife tikhoze kufulumira.

160 Tsopano, Yesu anadzizindikiritse Yekha, chizindikiritso cha Mwamalemba kwa Ayuda, kuti Iye anali Mesiya, pokhala mneneri. Nkulondola uko? Ameneyo anali Yesu dzulo, kwa mneneri, kapena kwa Ayuda.

161 Ndiye Amitundu sanali kumuyembekezera Iye. Ife tinali achikunja, tiri ndi chibonga pa nsana wathu. Ndipo ife tinkapembedza mafano, ife Amitundu. Ife sitinkamuyembekezera Mesiya aliyense, kotero Iye sanabwere kwa ife. Uthenga sunalalikidwe kwa—kwa—Amitundu kufikira Petro atasegulira Uthenga kwa iwo ku nyumba ya Kornelio, nthawi yayitali zitachitika zimenezo. Ndiyeno Paulo kenako anati, “Taonani, ine ndikutembenukira kwa Amitundu,” Ayuda atatha kumukana iye.

162 Zindikirani tsopano. Musaphonye ichi. Tsopano ichi chikuthandizani inu ngati inu muti mungomvetsera. Nchifukwa chiyani Iye sanachite chizindikiro ichi pamaso pa Amitundu? Iye anachita icho pamaso pa—Ayuda, Iye anachita icho pamaso pa Asamariya, koma palibe nthawi imodzi yomwe Iye anachita icho pamaso pa Amitundu. Koma Iye ananeneratu kuti icho chikanadzachitidwa pamaso pa Amitundu. Pakuti, chimene Mulungu ali, Iye sangasinthe. Ngati Iye anapereka chizindikiro chimenecho kuti adzizindikiritse Yekha pakati pa Ahebri ndi pakati pa Asamariya, basi iwo asanadulidwe kuchoka ku Uthenga, ndipo ife takhala nazo zaka thuu sauzande za kuphunzitsa kwa Baibulo, ndipo tsopano Amitundu afika ku mapeto awo. Ndi mapeto kwa ife. Ndiyeno ngati Iye angatilole ife kuti tingodutsa chiphunzitso cha Presbateria, Baptisti, Methodisti, kapena zina zotero, mwa wamba, popanda kudzizindikiritse Yekha bwinobwino pakati pathu monga Iye anachitira nthawi imeneyo, Iye wachita chinachake

cholakwika. Kotero Iye samalemekeza munthu, ndipo Iye anati Iye akanadzazichita izo.

¹⁶³ Tsopano penyani, “Monga izo zinali mmasiku a Sodomu,” ndi pamene Amitundu anawotchedwa, kuwotchedwa ndithu. Tsopano, Nowa, Iye anamutchula Nowa, awo anali makhalidwe a anthu, amene iwo analimo. Koma zindikirani Amitundu, moto usanagwe kuti uwawononge Amitundu, Achisodomu ndi Gomorah, ndi mizinda yozungulira imeneyo.

¹⁶⁴ Zindikirani Abrahamu, choyimira cha Mpingo, waufulu, Mpingo wauzimu. Loti, choyimira cha mpingo wofunda, mu Babeloni...kapena osati mu Babeloni; mu Babeloni lero, koma mu Sodomu nthawi imeneyo. Ndiyeno Achisodomu, osakhulupirira.

¹⁶⁵ Nthawizonse pamakhala mitundu itatu ya anthu. Ife—ife tiri nayo iyo pano, ife timakhala nayo iyo konsekonse. Amenewo ndi okhulupirira, odzipangitsa-kukhulupirira, ndi osakhulupirira. Ndipo ife timakhala nawo iwo konsekonse, ndipo magulu atatu a anthu.

¹⁶⁶ Mulungu amakhala wangwiro mu zitatu. Monga Atate, Mwana, Mzimu Woyera, zimapanga Mulungu mmodzi. Ndipo kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, zimapanga kubadwa kumodzi. Madzi, Magazi, ndi Mzimu, zimapanga Kubadwa kumodzi. Ndi zina zotero, mwaona, zonsezo, ndi zangwiro. Ife tiribe nthawi yoti tidutse a—mmawerengero a Mulungu, mwa Ake, mmene Iye amakhalamo wangwiro; ndi momwe Kudza Kwake kudzakhalire, ndi zina zotero, ndi chiwerengero chake, koma ife tiri mmenemo.

¹⁶⁷ Zindikirani tsopano pamene ife tikuwerenga, ife tapeza tsopano Amene, Mesiya uyu ali. Yesu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Nowa, ndipo monga mmasiku a Loti.” Tsopano Abrahamu ankayembekezera mwana wolonjezedwa. Chomwechonso ife tikutero. Mpingo woyitanidwa-utuluke, kuimirira anthu obadwa-mwatsopano amene adzipatula okha kwa dziko lapansi. Iwo siali mu Sodomu. Iwo ayitanidwa atuluke, ayikidwa kumbali, atanyamula lonjezo la Mwana amene akubwera.

¹⁶⁸ Ndipo, tsopano, tsiku lina pamene Abrahamu anali atakhala mdziko lowuma.

¹⁶⁹ Ndipo Loti akukhala ukulu wake... iye ayenera kuti anali meya wa mzindawo, woweruza. Iye anadzakhala munthu wotchuka. Mkazi wa Loti ankadula tsitsi lake ndi kumachita chirichonse chimene iye ankafuna kuti achite, ine ndikuganiza, kumusi uko ndi ena onse Achisodomu. Koma osati Sarah; ine ndimangoyenera kuti ndichiyike icho mmenemo, abale. Zindikirani, iye ankakhala momwe iye ankafunira kutero. Iye anali mkazi wotchuka kwambiri. Iye ankadana nazo kuti azisiye zimenezo.

¹⁷⁰ Koma osati Sarah. Iye anali kumtunda uko ndi mwamuna wake. Iye anaitanidwa atuluke, anasindikizidwa, ndi lonjezo lakuti iye akanadzakhala ndi kuchezeredwa kuchokera kwa Mulungu, mwana anali akubwera.

¹⁷¹ Ndipo chomwechonso Sarah-wauimira Mpingo lero, waitanidwa kutuluka, kuchokera ku Sodomu, uli ndi lonjezo loyembekezera Mwana wakudza. Ameni. Kulilola dziko kuti lichite chirichonse chimene ilo likufuna; izo ziribe chochita ndi iye. Iye akusunga malingaliro ake pa lonjezolo.

¹⁷² Chinachitika ndi chiyani? Abrahamu anadzutsa maso ake ndipo anayang'ana, ndipo iye anawona amuna atatu akubwera. Ndipo kodi inu munazindikira? Abrahamu, pamene iye anawona amuna atatuwo, iye anati, “Mbuye wanga, kodi Inu mungakhotere kuno?” Apo panali atatu a iwo. Iye anati, “Mbuye wanga,” mmodzi.

Pamene Loti anawona awiri a iwo, iye anati, “Ambuye anga.”

¹⁷³ Abrahamu ankadziwa chimene iye ankachikamba. Iye anati, “Mbuye wanga.” Atatu a iwo, ndipo, “Mbuye wanga.”

Loti anawaona awiri a iwo, iye anati, “Ambuye anga.”

¹⁷⁴ Kotero iye anati, “Mbuye wanga, dutsirani kuno.” Ndipo iwo anayima. Inu mukudziwa zokambiranazo.

¹⁷⁵ Zindikirani tsopano, Loti anali ali uko mu Sodomu. Ndipo Angelo awiri anapita uko mu Sodomu, kukalalikira Uthenga, kuti akawayitanire olungamawo kunjira kuchoka pakati pa osakhulupirira. Nkulondola uko? Billy Graham wamakono. Iwo sanachite zozizwitsa zambiri; anawakantha iwo ndi khungu, chimene, kulalikira kwa Mawu kumamukantha wosakhulupirira ndi khungu. Koma Billy Graham wamakono, mwangwiro.

¹⁷⁶ Ndipo kodi inu munayamba mwazindikirapo? Mwa amuna onse opambana amene ife takhala nawo mdziko, a alaliki, kuyambira mmasiku a Yesu Khristu; Sankey, Moody, Finney, Calvin, Knox, ena otero, kumapitirira ndi kumapitirira, ndi kumapitirira ndi kumapitirira, ife sitinayambe takhalapo konse ndi munthu mmenemo amene dzina lake limathera ndi h-a-m, monga Abraham, koma G-r-a-h-a-m. Koma zindikirani, zilembo sikisi, G-r-a-h-a-m, sikisi. A-b-r-a-h-a-m ndi seveni. Ife sitinakhalapo nazo izo konse, koma kuli mtumiki uko mu Sodomu, “Tulukani mmenemo.” Ndipo Mulungu watumiza munthu woyenera, Billy Graham, akuwayitana iwo kuchokera ku Sodomu. Ndipo iwo analandira chizindikiro cha kulalikira kwa Uthenga. Ndipo iwo akuwulandira Iwo lero, dziko lonse, mwa m'bale wodziwika, wofunika, Billy Graham, ali ndi uthenga wa chipulumutso, ndi, “Tulukani mu Sodomu!” Uko nkulondola. Ndi dzina lake lothera, *h-a-m*, kutanthauza kuti “atate wa anthu, kapena mafuko.”

177 Koma kunali Mtumiki, aponso, yemwe anatsala ndi Abraham, A-b-r-a-h-a-m. Ndipo zindikirani, monga Iye ananenera, Iye anawapatsa iwo chizindikiro.

178 Tsopano kumbukirani, dzina lake linakhala liri Abram, masiku angapo mmbuyomo; Sarai, osati Sarah. Dzina lake linakhala liri Abram, osati Abraham. Zindikirani, Mwamuna amene anakhala pansu ndi kumayankhula ndi iye, anati, “Abraham, alikuti mkazi wako, Sarah?”

179 Tsopano akazi mmasiku amenewo sanali monga iwo amakhallira lero, kumathamangira kunja ndi kumakalowerera mu geni ya mwamuna wake, ndi kumayendetsa geniyo ndi chirichonse. . . Mwaona, iwo anakhala kuseri kumene kunali kwawo. Koma, iwo, iye anakhala mu hema.

Ndipo Iye anati, “Alikuti Sarah mkazi wako?”

180 Tsopano penyani chimene Baibulo linanena. Abraham anati, “Iye ali mu hema, kumbuyo Kwanu.” Mngeloyo anali atatembenezira nsana Wake ku hema.

181 Ndipo Mngeloyo anali Munthu, chifukwa Iye anali atadya mnofu wa ng’ombe, anamwa mkaka kuchokera kwa ng’ombe, ndipo anadya nsima ina ndi batala. Uko nkulondola. Iye anatero. Iye anadya ndipo anamwa ndi Abraham, pamene iye anatenga chitsamba ndi kumaingitsa ntchentche pa Iye, pamene Iye anayima pamenepo ndikumamwa. Uko nkulondola, Munthu!

182 Ndipo Iye anati, “Abraham, Ine. . .” Ndipo uyo ndi mlowammalo waumwini, kenanso. “Ine ndidzakuchezera iwe molingana ndi lonjezolo.” Anali ndani Ameneyo?

183 Ndipo Sarah, akumvetsera, atatchera khutu, inu mukudziwa, iye anaseka mwachinunu, monga, mwakachetechete. [M’bale Branham akutsanzira—Mkonzi]. “Ine, mkazi wokalamba, wasinkhu wa zaka handiredi, makhalidwe a banja anasiya kwa zaka zambiri; ine kudzakhala ndi chisangalalo ndi mbuye wanga kenanso, powona kuti iye ndi wokalamba?”

184 Ndipo Mngeloyo, nsana Wake atawutembenezira ku hema, anati, “Nchifukwa chiyani Sarah waseka?” Amen!

185 Zindikirani pamene Mngeloyo anasowa ndikuchokapo, Abraham anamutcha Iye, “Elohim.” Wophunzira aliyense amadziwa kuti paliponse pamene ungowone chilombo chachikulu A-m-b-u-y-e, zimatanthauziridwa mu Chigriki, *Elohim*, “Mmodzi Wokwanira Zonseyo, Wamphamvuzonse Uyo,” Yemwe ali Yehova Mulungu. Ulemelero!

186 Munthu ananena kwa ine, “Kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti, mumakhulupirira kuti ameneyo anali Mulungu?”

187 Ine ndinati, “Abrahamu anayankhula ndi Iye, ndipo iye anamutcha Iye ‘Mulungu.’ Iye ankayenera kudziwa.” Oh, ndine

wokondwa kwambiri kuti ndikumudziwa Mulungu wonga ameneyo!

¹⁸⁸ Kodi Iye anachita chiyani? Chimene ine ndikuganiza kuti Iye anachita chinali... Inu mukudziwa, ife tinapangidwa kuchokera ku zipangizo sikisitini zosiyanasiyana za dziko lapansi, inu mukudziwa: petroleamu, ndi kuwala kwa mdziko, ndi potashi, ndi kashiamu. Ine ndikukhulupirira kuti Iye anangoti, “Ine ndamva za machimo amenewo. Ine ndibwera, ndipita kumusi kumeneko ndipo ndikayang’ana pa izo. Bwera kuno, Gabriele,” anasonkhanitsa kuwala kodzaza manja, ndipo, Phuu! “Lowa mmenemo. Ndipo bwera kuno, Woodworm,” ndipo, Phuu! “Lowa mmenemo.” Kenako anadzipezera Yekha limodzi. Bwanji? Iye ndi Mulungu.

¹⁸⁹ Ndine wokondwa kwambiri kudziwa. Kutu, tsiku lina ine mwinamwake sindidzakhala kanthu koma ndidzabwerera ku kuwala kwa dziko. Ine ndikhoza kusadzakhala kanthu mwa izo zomwe mukhoza kudzazipeza. Mafupa awa akhoza kudzavunda, koma Iye amalidziwa dzina langa. Tsikulina Iye adzandiyitana ine; ine ndidzabwera mmawonekedwe Ake.

Ameneyo ndiye Mulungu wathu. Abraham anamutcha Iye “Elohim.”

¹⁹⁰ Zindikirani, Yesu anati, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala pa kudza kwa Mwana wa munthu.” Atumikiwo adzakhala ali mu Sodomu; ndipo Mpingo woyitanidwa-utuluke udzalandira chizindikiro, cha chiyani? Mulungu kuwonetseredwa mu thupi la munthu. Ulemelero! Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndi chizindikiro kwa Mpingo wa Amitundu. Tsopano ndi nthawi yathu. Ndi ife oti tiziwone izo, lonjezo la Mulungu. Ife tikhoza kuyima pano kwa ora, mmbuyo ndi mtsogolo, kudutsa mu Lemba, ndi kuziluka izo pamodzi ndi kutsimikizira kuti izo nzolondola. Ndipo ili ndi oralo. Apa pali chizindikiro chotsiriza choti chiwonetseredwe. Ife tiri ku nthawi yotsiriza.

¹⁹¹ Bukhu la Chivumbulutso, Mmibadwo ya Mpingo, M’badwo wa Mpingo wa Laodikaya, mngelo wachiseveni ankayenera... Mu kuwomba kwa masiku a zimenezo, “chinsinsi cha Mulungu chikuyenera kutsirizidwa.” Ndipo ife tiri mu M’badwo wa Laodikaya; aulesi, ofewa, osati abwino, ofunda, ndipo ndicho chikhalidwe chimene mpingo wathu wa Chipentekoste wafikamo. Mulungu wagwedeza mphatso iliyonse imene Iye akanatha pamaso pa iwo.

¹⁹² Izo zikundikumbutsa ine, monga dona wamng’ono mu Louisville, kuno osati kale kwambiri. Iye anali ndi mnyamata wamng’ono, akuyendayenda, akuyesetsa kugwedeza zoseweretsa zazing’ono, ndipo mwana wamng’onoyo anangokhala ndi kumayang’ana. Ndipo anthu ankamuyang’ana iye. Ndipo iye anayamba kukuwa. Iye anapita kumeneko,

ena a akazi, ndipo anakamufunsa iye chimene chinali cholakwika. Anati, “Mnyamata wanga wamng’onyu watenga mliri pa iye.” Ndipo anati, “Iye sakumazindikira zinthu monga ana amayenera kumazindikirira, msinkhu wakewu.” Ndipo anati, “Ine ndinamutengera iye kwa adokotala, ndipo adokotala anati iye anali wabwinoko, koma,” anati, “iye siali.” Anati, “Ine ndikagwedeza choseweretsa chaching’ono ichi, mwana wamng’ono aliyense...Ndipo iye akumangokhala ndi kumangoyang’ana. Mwana aliyense amayenera kuzindikira icho ngati chidole, ndi kuchifikira icho, koma iye akumangoyang’ana.”

¹⁹³ Icho ndi chinachake monga mpingo wa Chipentekoste. Mulungu watumiza Oral Roberts, ndi china chirichonse, pozungulira, akugwedezera mitundu yonse ya mphatso ndi zinthu, kwa mpingo. Iye watsanulira Mzimu Wake. Inu mwayankhula mmalirime, mwanthauzira, munali ndi mphatso za uneneri, ndi china chirichonse.

¹⁹⁴ Ndipo izo zafika ku nthawi yakuti Yesu Khristu adzizindikiritse Yekha pakati pa anthu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, chimene chiti chidzakhale chizindikiro chotsiriza chimene chiti chidzagwedezedwe pamaso pa anthu. Kumbukirani, kanthawi pang’ono atatha mawonetseredwe a Mulungu amenewo mmawonekedwe a munthu, mu thupi, moto unagwa ndipo unadzanyeketsa Amitundu. “Ndipo monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.”

¹⁹⁵ Iye anadzizindikiritse Yekha ngati Mesiya, kwa Ayuda, pozindikira malingaliro amene anali mu mtima mwawo, poyankhula kwa iwo maina awo ndi zinthu zosiyanasiyana. Iwo anadziwa kuti ameneyo anali mneneri amene Ambuye Mulungu analonjeza kuti akanadzamudzutsa. Enieniwo, owonawo amene anakonzedweratu kwa icho, anachiwona icho.

¹⁹⁶ Ngati mulibe kalikonse mu mtima kolandirira izo, ndiye kuti mulibe kalikonse mmenemo. Inu mungapeze bwanji magazi kuchokera mu tanaposi? Mulibemo magazi mmenemo. Koteru munthu angakhoze bwanji kukhulupirira pamene mulibe chirichonse mmenemo choti akhulupirire nacho?

¹⁹⁷ Koma ngati Mzimu Woyera uli mmenemo, mwamsanga iwo umagwira Mawu amenewo. Iwo umawulukira kutali, mwaona, iwo umawatenga Iwo mwamsanga. Tsopano, “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Iye analonjeza apa kuti adzadzizindikiritse Yekha pakati pathu, mwanjira yomweyo imene Iye anachitira.

Tsopano inu mukuti, “Koma Iye angadzizindikiritse Yekha motani?”

¹⁹⁸ “Komabe kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Komabe inu mudzandiwona Ine,

pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu.” Ndi Mzimu Woyera umene umayankhula kudzera mmalirime ndi kupereka kutanthauzira, Mmodzi yemweyo amene amakupulumutsani inu ku tchimo. Ndi Yesu Khristu yemweyo, wabwera.

¹⁹⁹ [Mlongo akuyankhula mmalirime. Winawakenso akuyamba kuyankhula mmalirime. Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi]. Firii. [Malo osajambulidwa pa tepi.] Matamando akhale kwa Ambuye. Kodi inu munazindikira zimenezo? Kupitiriza kumati, “Tulukani, tulukani, tulukani,” mwaona, kuyitanira atuluke. Chabwino, inu mukumva chimene icho chiri.

²⁰⁰ Tsopano Baibulo limayankhula, ngati pali alendo ena pano, Baibulo limayankhula za kuyankhula ndi malirime ndi kutanthauzira, inu mwaona. Kotero ngati izo ziyankhulidwa mmalirime ndi kutanthauziridwa, ndiye kuti ndi ulosi. Mwaona, uko nkulondola, sichoncho izo? Ndi uneneri.

²⁰¹ Tsopano tulukani. Tsopano Ambuye akuwoneka kuti akunena kuti Iye akupatsani inu mwayi tsopano, mwaona, chinachake chimene inu simunayambe mwachiwonapo kale, chinachake chimene Iye ati achichite. Tsopano tiyeni tikhulupirire zimenezo ndi mtima wathu wonse.

²⁰² Tsopano ife basi, Billy ndi ine, pamene ife tinapita ku India ulendo wotsiriza uwu, ife . . . Ine ndiri ndi chidutswa chochokera mu pepala. Ndipo ilo linati, “Chi—chivomezi chikuyenera kuti chatha.” Masiku pang’ono ife tisanafike kumeneko, iwo anadziwa . . . Mwaona, India ilibe mipanda monga inu muli nayo kuno, mipanda ya waya. Iwo amatola miyala, ndipo iwo amamangira nyumba zawo zambiri. Iwo ndi anthu osawuka kwenikweni. Ndipo—ndipo mbalame zazing’ono zimamanga zisa zawo mmiyala imeneyi, ndiyeno ng’ombe ndi nkhosa zimabweramo, madzulo, ndi kudzayima mozungulira makoma amenewa, pamene dzuwa likuwala, kuti zikhale pamthunzi.

²⁰³ Koma iwo anazindikira, kwa masiku angapo, ng’ombezo sizinabweremo, izo zinangokhala kunja komwe mmunda. Nkhosazo zinasonkhana pamodzi ndi kukumbatirana ina ndi imzake, ndipo zinatsamirana ina ndi imzake, m’mundamo, kuti zimve kuzizira. Mbalame zonse zinawuluka kuchoka ku makomawo. Izo sizinkadziwa chimene chikanati chichitike. Kenako chivomezi chinakantha, ndipo icho chinagwetsera makomawo pansi. Kenako mbalame zazing’onozo zinabwereranso ndipo zinadzamanga zisa zawo kachiwiri mu milu ya miyalayo, ndipo ng’ombezo zinayamba kubwera kachiwiri.

²⁰⁴ Tsopano, penyani, ngati uyo sali Mulungu yemweyo amene anakhoza kuzichenjeza izo kuti zikalowe mu chingalawa, mmasiku a Nowa! Ndipo ngati Mulungu anakhoza kuchita zimenezo, ndi kuzichenjeza mbalame, mwa kununkhitsa; ndi kuzichenjeza ng’ombe ndi nkhosa, mwa kununkhitsa,

kuti zichoke ku makoma aakulu akale awo amene akanati agwe. Mulungu akuyesetsa kuti awachenjeze anthu Ake lero, kuti achoke ku makoma akale achipembedzo awa omwe ati adzagwere mkati, limodzi la masiku awa, pakuti Kudza kwa Ambuye kuli pafupi.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

²⁰⁵ Ambuye Yesu, ine ndikumverera kuti ndi nthawi yoti ine ndiyime tsopano. Ndipo ndi nthawi Yanu yoti muyankhule, Atate. Ine ndayesetsa kuwauza anthu kuti Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndayesetsa kutsimikizira izo mwa Malemba, chimene Inu munali, ndi momwe Inu munadzizindikiritsira Nokha.

²⁰⁶ Ndiye ine ndikukumbukira kachiwiri, mu Yohane Woyera mutu wa 14 ndi ndime ya 12, Inu munati, “Iye amene akhulupirira,” osati kudzipangitsa kukhulupirira, “iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndizichita nayenso adzazichita.” Izo zingachite motani chinachakenso, Atate? Ngati ife tingasamutse moyo kuchokera ku mtengo wa peyala kupita ku mtengo wa pichesi, iwo ungabale mapeyala, pakuti moyo wa mtengo wa peyala uli mu pichesi. Ndipo, Atate Akumwamba, ngati Moyo umene unali mwa Khristu, malingaliro amene anali mwa Iye, Mzimu umene unali mwa Iye, walonjeza kuti udzakhala mwa ife, ndiye ife tikuchitira umboni za zimenezo. Ngati Iye ali Mpesa ndipo ife ndi nthambi, Moyo umachokera ku Mpesa. Ambuye, mutilole ife tikhale nthambi, usikuuno. Ife tikuzindikira kuti mpesa sumabala chipatso chirichonse; iwo unachokapo, koma iwo unabwereranso mmawonekedwe a Moyo, ndipo nthambi zimabala chipatso. Liwu Lanu ndi pamene Inu muyankhula kudzera mwa ife. “Ngati inu mudzanena kwa phiri ili suntha, ndipo osakayika mu mtima mwanu, koma kukhulupirira kuti chimene inu mwanena chichitika, inu mukhoza kukhala ndi chimene inu mwanenacho. Pamene inu mupemphera, mukhulupirire kuti mwalandira chimene inu mwachipemphacho, icho chidzaperekedwa kwa inu.” O Mulungu, malonjezo oterowo! “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndipo Mawu Anga nkukhala mwa inu, ndiye pemphani chimene inu mukuchifuna.”

²⁰⁷ O Mulungu, malonjezo oterowo amene mpingo uli nawo, ndi chiwombolo changwiwo choterocho! Ife tikuzindikira kuti sitiri oyenera, ndipo ife sitidzakhala konse oyenera. Palibe njira yoti ife tingakhalire oyenera. Ndipo ife sitikuwerengera kuyenera kwathu. Ife tikuyang’ana ku Nsembe yathu, Ambuye Yesu. Iye ndi Yemwe ife tabisalamo, usikuuno. Ife tatetezedwa mu lonjezo Lake lodala, mu Mawu Ake. Icho ndi chathu. . .

²⁰⁸ Awo ndi malo obisalilapo achikhulupiriro, pa Thanthwe losasunthika la Mawu Amuyaya a Mulungu. Chikhulupiriro chimatenga ake—malo ake pomwepo, malo ake, palibe chimene

chingasunthe icho. Imfa siingathe kuchigwedeza icho. Manda sangathe kuchibisa icho. Izo zatsimikiziridwa. Pa tsiku lachitatu Iye anauka, chifukwa Mawu a Mulungu anati, “Ine sindidzasiya solo Yake mu gehena, ngakhalenso sindidzalola woyera Wanga kuti awone chivundi.” Palibe manda amene akanakhoza kumugwira Iye.

²⁰⁹ O Mulungu, ndi Mawu Anu. Apangitseni iwo kuti awonetseredwe usikuuno. Inu ndi Mawu. Ndipo mulole kuti Mawu amene Inu munalonjeza, ayankhulidwe usikuuno, Ambuye, ndipo mulole kuti chizindikiro chakuti Mesiya ali pa dziko lapansi, ndipo ife tiri ku mapeto a nthawi. Monga amuna anzeru aja anawona nyenyezi zitatu zikufola, kuti zikhale imodzi; ndipo pamene ife tikuwona, lero, Ambuye, zikhumbo zitatu za Mulungu potsiriza zikufika mu mpitawo, ife tikudziwa kuti izo ndi chimodzi. Ndipo ife tikuwona zizindikiro zazikulu zonsezi pa dziko lapansi, zimene zikuwonekera; ndi chizindikiritso cha Mwana wa Mulungu, akuchita mu thupi la Mpingo Wake, kuti azipitiriza ntchito Yake. Mulungu, mulole kuti mitima ya anthu injenjemere. Mulole kuti ochimwa anjenjemere. Ndipo mulole kuti pakhale kulapa, ndipo mulole kuti pakhale machiritso otero, usikuuno, a zonse ziwiri solo ndi thupi, kuti amuna ndi akazi, kulikonse, achoke ku kusakhulupirira, adzilekanitse okha ndipo akhulupirire pa Mulungu wamoyo.

²¹⁰ Ine ndikudzipereka ndekha kwa Inu, Ambuye, ngati wantchito Wanu. Ine ndikuwupereka mpingo uwu kwa Inu. Ine ndikuzindikira, Ambuye, ziribe kanthu ndi mochuluka bwanji momwe Inu mungati mundidzozere ine, ngati anthu sakhulupirira izo, ndiye izo sizingachitike. Ife tonse tikuyenera kugwira ntchito limodzi ngati thunthu la chikhulupiriro cha Mulungu, ndi la ulemu wa Mawu a Yesu Khristu, kuti tiwone zinthu izi zikuchitika.

²¹¹ Ife tafunsidwa funso, “Mabwana, ife tikufuna kumuwona Yesu.” Ndipo, Atate, Inu munalonjeza kuti, kuti Inu mudzakhala nafe. Tsopano ife tiyembekezera pa Inu kuti muwonekere pakati pathu, Ambuye. Mu Dzina la Yesu Khristu ine ndikupempha zinthu izi. Amen.

²¹² Tsopano ine ndikukhulupirira...ndipo ngati makadi a pemphero anaperekedwa. Wani mpaka handiredi? Chabwino, tiyeni, ife sitingathe kuwayimitsa iwo onse pa nthawi imodzi, ife tikungoyenera kuti tidziwatenga iwo mmodzi ndi mmodzi. Tsopano pamene...Ife tizikuitanani inu, mmodzi ndi mmodzi, ndiyeno ngati inu muli olumala, opuwala, simungathe kuimirira, ena a abalewa abwera, akubweretsani inu ku nsanja, kuti mudzapemphereredwe.

²¹³ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]...imani. Ngati inu simungathe, mundidziwitse ine. Nambala thuu, khadi la

pemphero nambala thuu, kodi inu mungaimirire. Zikomo inu.

²¹⁴ Nambala firii, ndani ali ndi khadi la pemphero nambala firii? Kodi inu mungaimirire? Mwachangu ndithu tsopano, ife tikuyenera kuti tifulumire. Kodi dona uyu, kodi iye ali ndi nambala firii, khadi la pemphero? Chabwino. Chabwino, pitani kumusi ku mapeto kumusi uko, nambala firii. Billy, iwe kapena winawake abwere kuno.

²¹⁵ Nambala foro, nambala foro, khadi la pemphero nambala foro, ndani ali nalo ilo? Kumbuyo komwe uko. Chabwino, bwerani kuno, dona. Nambala faivi. Inu nonse muitanidwa, mmodzi ndi mmodzi. Nambala faivi.

²¹⁶ Kodi inu muli ndi khadi lanji, bwana? [M'baleyo akuti, "Nambala firii, B."—Mkonzi]. Nambala chiyani? ["Firii."] Nambala firii? Winawake walakwitsa. Uyu—bambo uyu apa ali ndi khadi nambala firii. Chabwino.

²¹⁷ Nambala foro, ndani ali ndi nambala foro, khadi la pemphero nambala foro? Chabwino, nambala faivi, ndani ali ndi khadi la pemphero nambala faivi? Nambala sikisi, ndani ali nalo ilo, nambala sikisi? Zikomo inu. Bwerani. Nambala seveni. Tsopano muzingotenga malo anu. Nambala seveni. Nambala eyiti, eyiti.

²¹⁸ Naini, naini, kodi ine ndinaliwona ilo? Naini, winawake afulumire tsopano kuti ife tibatenge nthawi yochuluka pa iwo. Nambala naini, khadi la pemphero nambala naini, chonde. Winawake andithandizire ine kuyang'ana. Kodi abale inu mungaimirire ndi kundithandizira ine kuyang'ana. Nambala naini, palibe pano? Chabwino, ngati ilo litabwere, ilo likhoza kudzatenga malo ake; mwina watuluka, ine ndinalalikira motalikitsa.

²¹⁹ Nambala teni, khadi la pemphero teni, kwezani mmwamba dzanja lanu kuti ife tikhoze kuwona yemwe inu muli. Chabwino, bwerani. Leveni, khadi la pemphero leveni. Kodi inu munalibe ilo, dona? Muzikweza manja anu pamene ine ndikuuzani inu, ndiyeno inu, pamene nambala yanu yaitanidwa, ndiye inu—inu mudziwa.

²²⁰ Nambala thwelovu, nambala thwelovu, ndani ali nalo ilo? Nambala thwelovu. Bwerani, dona. Nambala sartini, khadi la pemphero sartini. Kumbuyo komwe uko. Bwerani, dona, ngati inu mungathe kuimirira. Nambala sartini. Nambala fortini, nambala fortini, kodi lili pati? Khadi la pemphero fortini, kumbuyo komwe uko. Chabwino, bwerani patsogolo, dona. Nambala fifitini, bambo uyu pomwepa, nambala fifitini. Sikisitini, sikisitini, sikisitini, khadi la pemphero nambala sikisi- . . . Uko pa kona. Seventini.

²²¹ Mwaona, ili si bwalo lamasewera, ife sititero. . . Ife—ife timawayitana iwo, mmodzi ndi mmodzi; inu mulibe mpikisano waukulu wopitirira ndi kumadumphiramo, inu mukudziwa. Ife tikufuna dongosolo, mwaona, kulemekeza.

222 Nambala sikisitini, khadi la pemphero nambala sikisitini. Nambala sikisitini, kodi dona uyu ali ndi sikisitini? [M'bale akuti, "Fortini."—Mkonzi]. Fortini. Nambala sikisitini, sikisitini. Chabwino, zikomo inu, bwana. Nambala seventini. Ali kale kuno, eya, seventini. Eyitini. Chabwino. Eya.

223 Chabwino, iwo afika kale ochuluka kumeneko amene angathe kuyima pa kona pa nthawi ino. Ife tiyamba, mu maminiti pang'ono okha, kuchokera pamenepo. Chabwino.

224 Ndi angati a inu, pamene iwo akuwafoletsa anthu amenewo, amene mulibe khadi la pemphero, tiyeni tiwone manja anu, ndipo inu mukudwala? Chabwino, pamene ine ndikubwereza Lemba kwa inu. Tsopano inu mulibe khadi la pemphero, komabe inu mukudwala, inu simuyitanidwa mu mzere wa pemphero? Chabwino.

225 Ndi angati mchipinda chino amene simukundidziwa ine, ndipo mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani mmwamba manja anu; amene mukudwala, inu mukudziwa. Mukuona? Kuti ndikhale woonamtima ndi inu, ine sindikumuwona munthu mmodzi yemwe ine ndikumudziwa. Tsopano, inu mukhoza kundidziwa ine, koma moonamtima... Ine—ine sindikutanthauza izi kudzera mu kupweteka kulikonse, ine sindinakuwonenipo inu, ndipo ine—ine—ine sindiri, ine sindikutha kumuwona munthu mmodzi amene ine—ine ndikumudziwa, kupatula ngati ali munthu wamng'ono wokhala ngati wojintcha uyu wakhala pamenepo, wamng'ono... Kodi ine ndikuyang'ana pa munthu wolondola? Ine ndaiwala kuti dzina lanu ndi ndani, ndinu wochokera ku Missouri. Ine—ine ndikudziwa iye amabwera ku kachisi kamodzi pakapita kanthawi.

226 Tsopano, ndipo pa nsanja, tsopano, kumbukirani, Mulungu ali basi mochuluka pa nsanja mmene Iye alirinsu kunja uko. Ine sindikumudziwa aliyense pano, kuti ndingonena kuti ine ndikuwadziwa iwo, kupatula m'bale yemwe ali pomwe pano, ndi M'bale Moore, kuti ndidziwe kwenikweni dzina kapena kumudziwa aliyense. Ine ndikhoza kudziwa... Ine—ine ndikuganiza awa ndi abambo ako akhala kumbuyo uko, ine ndikutsimikiza ndithu kuti uko nkulondola. Ndipo Jim Maguire apa, a—mnyamata wa tepi wakhala apa. Ndipo ndiwo onse amene ine ndikuwawona, kuwadziwa, ndi kudziwa yemwe iwo ali. Chabwino.

227 Mvetserani, tiyeni tingotenga kankhani kakang'ono monga aka pamene iwo akukonzekera, nkhani ina imene ife tingakhoze kuyitenga yokhudza Ambuye Yesu. Apa, ndi angati akudziwa kuti Baibulo limanena kuti nthawi yina kunali mkazi amene anali ndi vuto la magazi? Ndipo iye sakanakhoza, iye sanayitanidwe mu mzere wa pemphero, nayenso. Koma, ndipo iye analibe khadi la pemphero, koma iye anali ndi

chikhulupiro, ndipo icho ndi chimene chimamukhudza Mulungu. Ndipo Yesu akupita mu msewu, mkazi wamng'ono uyu anazembera mkati ndipo anadzakhudza mphonje ya chovala Chake.

²²⁸ Ndi angati akudziwa kuti chovala chaku Palestina chimakhala chomasuka? Unali mkanjo. Ndipo iwo unkakhala ndi chovala chamkati, nawonso, mwaona, kuti chizichotsa fumbi pa miyendo yawo. Kotero iwo ankakhala—iwo ankakhala ndi chovala chamkati, chovalacho chinkatenga fumbi pamene iwo akuyenda. Ndipo kotero iwo ankakhala ndi chovala chamkati.

²²⁹ Ndipo mkazi uyu anakhudza mphonje ya chovala Chake, ndi chala chake. Ndipo Yesu anayima, ndipo Iye anati, “Ndani wandikhudza Ine?” Ine sindikukhulupirira kuti Iye ankangoseleula. Ine sindikukhulupirira kuti Iye anachita zimenezo. Ine ndikukhulupirira moona kuti Iye sankadziwa yemwe anachita izo. Iye anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

²³⁰ Ndipo mochuluka, anthu ambiri anali ndi mikono yawo atamukumbatira Iye, “Moni, Rabbi! Kodi uyu ndi Mneneri waku Galileya? Chabwino, ndife okondwa kukuwonani Inu kuno.” Aliyense, “Inu muli bwanji?”

²³¹ Petro anati, “Ambuye!” Iye anamudzudzula Iye, Baibulo linatero. Mwa kuyankhula kwina, Petro akhoza kukhala kuti ananena izi, “Bwanji, izo zikumveka mwachirendo, kwa Munthu wa kayimidwe Kanuko kuti aziti ‘ndani anakukhudzani’ Inu. Ndipo ine ndikuganiza kuti, kuyambira pamene ine ndakhala ndikuyankhula ndi Inu, pakhala pali manja fifite akukukhudzani Inu. Ndiyeno Inu mukuti, ‘Ndani wandikhudza Ine?’ Bwanji, izo sizikumveka bwino mwa kuganiza, Ambuye. Inu simukuyenera kunena chinthu chonga chimenecho.” Baibulo linati, “Petro anamudzudzula Iye.”

²³² Koma Yesu anati, “Ine ndazindikira kuti ukoma wachoka mwa Ine.” Uko kunali kukhudza kwa mtundu wosiyana, kukhudza kwa chikhulupiro. Ukoma ndi mphamvu. “Ine ndazindikira kuti mphamvu Zanga. . . Ine ndafooka. Winawake wandikhudza Ine ndi—kukhudza kwa chikhulupiro.”

²³³ Tsopano Iye sakanakhoza kuzimverera izo, mwathupi. Inu mukhoza kukhudza chikhotho changa, ndipo zinalipo zochuluka kwambiri pakati pa mphonje ya chovala Chake ndi thupi Lake, kuposa zomwe ziri ku chikhotho changa.

²³⁴ Chimodzimodzi monga Bartumeyo wakhungu, atayima mayadi handiredi kuchokera kwa Iye, anati, “Yesu, Inu Mwana wa Davide.”

²³⁵ Ndipo anthu onsewo akukuwa, “Ife tikumva kuti Inu munaukitsa akufa. Ife tiri ndi manda odzaza ndi iwo kuno. Bwerani kuno ndipo mudzawadzutse iwo, ife tikukhulupirani Inu.” Mwaona, otsutsa amenewo, mwaona, ndi zina zotero.

Koma Yesu sanamumve nkomwe Bartumeyo, koma chikhulupiriro chake chinamuimitsa Iye. Mwaona, chikhulupiriro chake chinachita zimenezo.

²³⁶ Tsopano, chikhulupiriro cha mkazi uyu chinamuyimitsa Iye, ndipo Iye anayang'ana pa unyinjira wonsewo mpaka Iye anamupeza mkazi wamng'onoyo. Ndipo Iye anamuiza iye za vuto lake, ndipo anati, "Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe." Nkulondola uko? Basi mkazi wamba wamng'ono, wooneka mofooka, ndipo iye anachiritsidwa.

²³⁷ Tsopano kodi iye anachita chiyani? Iye sanamukhudze konse Iye, ndendende. Iye anamukhudza Mulungu, kudzera mwa Iye. Chabwino, ndiye ndizo. . . Ndi angati akudziwa. . . Atumiki awa, chimene, ine ndikudziwa kuti iwo akudziwa. Koma Bukhu la Ahebri limanena kuti, "Yesu Khristu tsopano ndi Wansembe Wamkulu amene akhoza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zifooko zathu." Nkulondola uko?

²³⁸ Ndi angati akudziwa zimenezo mwa omvetsera? Chabwino, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu, Iye ndi Wansembe Wamkulu yemweyo amene Iye anayamba wakhalapo. "Palibe mkhalapakati wina pakati pa Mulungu ndi munthu, koma Munthuyo Khristu Yesu." Ndiye ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndipo inu mukamukhudza Iye mwanjira yomweyo imene iye anachitira, ndipo Iye akhoza kukhudzidwa, ndipo ngati inu mungamukhudze Iye mwanjira yomweyo imene iye anachitira, kodi Iye sangachite mwanjira yomweyo mmene Iye anachitira nthawi imeneyo, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Nkulondola uko? Eya? Chinthu chokhacho chimene inu mukuyenera kuchita ndi mukukhudza Iye.

²³⁹ Tsopano, osati kukhudza mmodzi wa abale athu, kapena kundikhudza ine. Awo, awo ndi abale anu chabe, inu mwaona. Koma mukukhudze Iye. Chikhulupiriro chanu chimukhudze Iye, ndiye Iye agwiritsa ntchito chida Chake ndipo Iye akhala. . . Iye achita zomwezo lero zomwe Iye anayamba wazichitapo. Iye ali yemweyo basi lero, ndi kwanthawizonse. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo?

²⁴⁰ Kotero tsopano ine ndikufuna inu nonse, tcheru chanu chosagawanika, munthu aliyense akhale mmalo mwake kwa maminiti ochepa otsatirawa, ndipo apemphere.

²⁴¹ Tsopano, ndi chinthu chopambana kubwera kuno ndi kudzalalikira Uthenga umene ungawapangitse anthu, kwenikweni, amene nthawiyina anali zidakhwa ndi anjuga, ndi mahule ndi china chirichonse, kunja pa msewu, kuti akhale mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, ndi kumakhoza kumverera kudzoza kwa Mzimu kuti ukukwezereni inu pa malo mpaka inu kudzitaya nokha, ndi kufuula "ameni" ndi "aleluya," matamando kwa Mulungu. Ichu ndi

chinthu chopambana. Komano mwa omvetsera omwewo, ndipo Uthenga ukulalikiwa ndi kunena chimene Iye anali, tsopano kumuzindikiritsa Iye kachiwiri kubwereranso Mmodzi yemweyo.

²⁴² Tsopano mu mzere wa pemphero uwu wayima apa, ine sindikuganiza. . . Ine sindikumuwona munthu mmodzi mu mzere umenewo amene ine ndikumudziwa. Palibepo munthu. Ngati aliyense wa inu amene muli mu mzere wa pemphero uwo, muli alendo kwa ine, ine sindikukudziwani inu, inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Aliyense wa inu mu mzere wa pemphero, amene mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Ine ndikuganiza, iwo unali mzere wonsewo wa pemphero. Tsopano, ine sindikumudziwa aliyense wa iwo. Tsopano njira yokhayo imene. . .

²⁴³ Ndipo ngati aliyense akuganiza kuti izi ndi zolakwika, inu mubwere kuno ndipo mudzatenge malo anga. Mukuona? Mpaka inu mutachita chinthu chomwecho, ndiye musanene kanthu za izi. Yesu anati, “Ngati ine ndikutulutsa ziwanda ndi chala cha Mulungu, ana anu amatulutsa izo ndi ndani?” Mwa kuyankhula kwina, “Ndi kachitidwe kanji kamene iwo ali nako kabwinoko?” Mukuona?

²⁴⁴ Tsopano ife takhala nayo nthawi imene aliyense amayamba kulingalira za mwambo wakale, kusanjika kwa manja. Ndipo izo ndi zabwinobwino. Koma tsopano, abale anga otumikira, mungondichitira ine umboni, umenewo unali mwambo wa Chiyuda. Mukuona?

²⁴⁵ Yairo anati, “Bwerani mudzaike dzanja Lanu pa mwana wanga wamkazi, ndipo iye akhala moyo.” Koma Wachroma, Wamitundu, anati, “Ine siwoyenera kuti Inu mubwere pansu pa denga langa. Mungoyankhula mawu.” Nkulondola uko? Ndi mawu oyankhulidwa; Amitundu, mwaona. Ife tikuyenera kumachita zimenezo; ngati Mroma ameneyo anaganiza zimenezo, wachikunja amene anali atangomuwona Iye. Chifukwa, iye ankadziwa zimenezo, Mawu a Yesu Khristu. Iye anati, “Ndine munthu wa ulamuliro. Ine ndikanena kwa munthu *uyu*, ‘pita,’ ndipo iye amapita, ndipo *uyu* amabwera. Iye akuyenera kutero, chifukwa iye ali pansu pa ine.” Kodi iye ankazindikiritsa chiyani? Kuti matenda aliwonse ndi nthenda iliyonse zinali pansu pa ulamuliro wa Yesu Khristu. Inde, bwana. Iye ali ndi ulamuliro.

²⁴⁶ Ndipo ngati ife tingamumve Iye akuyankhula, ndiye izo zimuzindikiritsa Iye kuti ali ndi ife. Zingakhale zazikulu bwanji kwa inu Amitundu, usikuuno, kuti mudziwe, ndi kudziwa kuti Iye ali pakati pathu, ndipo akhoza kufikira ndi kuzindikira. Osati kuti, “M’bale Branham anayika manja pa ine; M’bale Roberts, kapena wanga. . . winawakenso.” Koma

mwa chikhulupiriro mwa Mwana wa Mulungu, kuti, “Ine ndikukulandirani Inu, Ambuye Yesu. Inu muli pano. Inu mundichize ine.”

²⁴⁷ Tsopano ngati Iye ati adzizindikiritse Yekha ndi kutsimikizira mwa Uthenga kuti Iye ali basi mochuluka pano tsopano monga Iye anali nthawi imeneyo. Ine ndatsimikizira kwa inu, kuti icho ndi chilemba Chake chozindikiritsa, (nkulondola uko?) analonjeza mmasiku otsiriza kuti zinthu izi zikanadzachitika. Ndipo ife tawuwona mpingo ukupita kumene mwa izo kudzera mwa Luther, Wesley, Pentekoste, ndi mpaka kumapeto komwe. Mukuona? Ndipo apa ife tiri, M’badwo wa Laodikaya, M’badwo wa Sodomu, ndipo ndife pano. Utumikiwu wabwera kudzera mu ngodya iliyonse ya Mawu. Ndipo ine ndikukhulupirira, chinsinsi chonse cha Mulungu, Ichu chalalikidwa kale. Tsopano ndi kuzindikiritsidwa kwa Khristu pakati pa anthu Ake, Mulungu akugwira ntchito mu mnofu wa munthu.

²⁴⁸ Tsopano, ziribe kanthu kuti ndimochuluka bwanji momwe Iye angandidzozere ine, inu mukuyenera kuti mudzozedwe, nanunso, kuti mukhulupirire zimenezo. Mwaona, inu ndi amene mukuyenera kuchita kukhudzako. Mukuona? Ndipo awiri tonse a ife, pamodzi, tapanga thunthu. Ine sindikukudziwani inu; inu simukundidziwa ine. Inu mukangokhulupirira, ndipo ine nkukhulupirira, ndiye Mulungu atitenga ife tonse mdzanja. Ameneyo ndi Mulungu.

²⁴⁹ Ndiye, mwaona, Baibulo linati, “Ngati inu nonse muyankhula ndi malirime, ndipo apo nkubwera mmodzi pakati panu, amene ali wosaphunzira, popanda wotanthauzira, ndiye iye angati ‘Ndinu amisala.’ Koma mulole wina anenere ndi kuwulula chinsinsi cha mtima, ndiye onse a iwo adzagwera pansu ndi kuti, ‘Mulungu ali ndi inu.’” Ndine wothokoza kuliwona tsiku limenelo likufika, kukhala moyo sindikalika mokwanira kuliwona ilo pakati pa mpingo woyitanidwa-utuluke.

²⁵⁰ Inu mukukumbukira, izo sizinapite ku Babeloni. Izo sizinapite ku Sodomu. Izo zinapita kwa oyitanidwa-atuluke, Osankhidwa; ndicho chizindikiro chimene iwo anachiwona. Iwo ali nawo awo kunja uko, magulu awo a bungwe ndipo akumapitirira.

²⁵¹ Koma uyu ndi Ambuye Yesu Khristu mmawonekedwe a Mzimu Woyera, akuyenda pakati pa anthu Ake, akuchita chinthu chomwecho chimene Iye ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, akudzizindikiritsa Yekha ndi Mkwatibwi Wake, osati mpingo.

²⁵² Pali kusiyana pakati pa mpingo ndi Mkwatibwi. Osati kulalikirira chiphunzitsa, chifukwa ine sindimachita zimenezo; koma, kwa chikhulupiriro changa chodzichepetsa, Mkwatibwi akupita kudutsa a...kapena, a—mpingo ukupita kudutsa mu

chisawutso, chisindikizo chachisikisi, kuti chiwuyeretse iwo. Uko nkulondola. Koma Mkwatibwi satero; iye akupita mu Mkwatulo izo zisanachitike. Ndi nthawi yoti Mkwatibwi ayitanidwire kunjja, kotero tsopano ine ndikukhulupirira kuti ino ndi nthawi yoitanira-atuluke.

²⁵³ Mundikhululukire ine, abale, ine sindikuyenera kulalikira chiphunzitso, iwo akhoza kukhala...?.. Mukhoza kusagwirizana nazo; ngati inu mukutero, mungokhala ngati kudya chitumbuwa cha nthudza, mutaye njereyo ndi kudya chitumbuwacho. Inu mwaona, uko nkulondola. Chabwino.

²⁵⁴ Koma ine ndikukhulupirira kuti pamene ndi pamene ife timalakwitsira, pamene ena a ife timakhulupirira, wina, amati Iwo udzadutsa. Ndipo winayo nkumati, zedi, mpingo udzadutsa mu izo; koma, zedi, ndi umenewo mpingo uko mu Babeloni, kunjja uko mu Sodomu. Mkwatibwi waitanidwa atuluke, wakhala apa akumuyembekezera Mwana wakudzayo. Uko nkulondola. Inde, bwana. Uko ndi kumene chizindikirocho chikuchitidwa, osati kumusi pakati pa—zipembedzo; mwa osankhidwa.

²⁵⁵ Tsopano, pamaso pa Mulungu, pa Yemwe ine ndikuyimapo, ndipo sindikunama, Iye pokhala Woweruza wanga, mwaulemu ine ndikunena kuti palibe munthu mu mzere umenewo, monga ine ndikukumbukirira amene ndinamuwona konse mmoya wanga. Palibepo munthu, kupatula iwo amene ine ndawatchula kuno, amene ine ndikudziwa chinthu chimodzi cha iwo, kapena ndinayamba ndawawonapo; ndiri ndi Baibulo pano patsogolo panga.

²⁵⁶ Tsopano, ngati Yesu ali yemweyo dzulo ndi kwanthawizonse, monga ine ndakuuzirani inu! Ndipo inu mukudziwa kuti sindine wazafioleje, sindine mlaliki, monga mmene ine ndingatchulire monga azibusa anu apa odzozedwa kuti azilalikira izi. Awo ndi maitanidwe awo. Awa ndi maitanidwe anga, tsopano kudzozedwa ndi Mzimu Woyera, kumulola Mulungu kuti ayende kudzera mwa anthu Ake. Mukuona?

²⁵⁷ Tsopano kodi inu mukhulupirira zimenezo? Ngati Iye ati adziwonetsere Yekha pakati pa anthu Ake usikuuno, kuti Iye analonjeza, “Kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso Ine. Osakhulupirira sadzandiwonanso Ine. Ayi, iwo ali kunjja uko mu Sodomu. Koma inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu. Ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita. Zochuluka kuposa izi inu mudzazichita.”

²⁵⁸ Ine ndikudziwa kuti la King James limati, “zochuluka,” koma inu mupeze Emphatic Diaglott ndipo muwone ngati ilo silimati—silimati... King James amati, “zazikulu kwambiri.” Inu simungakhoze kuchita zazikulu kwambiri. Palibe chimene chingachitidwe mokulirapo. Iye anachiritsa odwala, anawukitsa

akufa, anayimitsa chirengedwe, anachita chirichonse chimene chinalipo. “Koma *zochuluka* inu mudzazichita.”

²⁵⁹ Chifukwa, Iye anangoimiridwa mwa munthu mmodzi pamenepe, Yesu Khristu, Mulungu. Koma tsopano Mulungu ali pakati pa Mpingo Wake, konsekonse. “Zochuluka kuposa izi inu mudzazichita, pakuti Ine ndikupita kwa Atate; kuti ndidzabwererense mmawonekedwe a Mzimu, Atate Mzimu.” Lawi la Moto lomwelo limene linkawatsogolera ana kudutsa mchipululu, limene linkakhala mwa Yesu Khristu, linabwereranso kwa Mulungu, ndipo anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndipo ndikupita kwa Mulungu.”

²⁶⁰ Zindikirani zomwe zinachitika mwamsanga pamene Iye anachita zimenezo. Saulo waku Tariso, ali panjira yake akupita, anakanthidwira pansu ndi Kuwala kwakukulu kuja, monga ine ndinanenera usiku watha. Iye anadziwa kuti ameneyo anali Ambuye. Iye anati, “Ambuye, Inu ndi Ndani?”

Anati, “Ine ndi Yesu.” Mukuona?

²⁶¹ Apo pali Lawi la Moto lomwe lija, Kuwala komwe kuja pakati pathu, likubereka Moyo umene Ilo linachita pamene Ilo linali mwa Khristu Yesu, likuchita chinthu chomwecho mu Mpingo wa Mkwatibwi lero. Mukuona? Kodi inu mukhulupirira zimenezo?

²⁶² Tsopano Ambuye Mulungu abwere ndipo adzayankhule za chimene ine ndinayankhula za Iye. Chikhulupiriro chophweka chimenecho, tsopano, Mulungu Kumwamba akudziwa, mwaona, kungokhulupirira zimenezo. Pamene Iye anakomana nane kumtunda uko, Iye anandiuza ine zimenezo. Ndipo apa ine ndayima usikuuno, ine ndayima, ine ndikuganiza kuti muli anthu firii—firii handiredi, kapena kupitirirapo, muno. Ndipo ine—ine—ine ndayima pamaso pa theka la milioni, ndi kupanga chitsutso, kuzungulira dziko lapansi. Ndipo Iye sangatero, Iye satero. . . Iye ndi Mulungu. Ichi, si chimene ine ndachinena, ndi chimene Iye ananena. Ndi Mawu Ake.

²⁶³ Tsopano ine ndikufuna kuti aliyense akhale molemekeza basi, pamene a. . . izo zikuchitika, ngati izo zingatero. Tsopano, ngati izo sizitero, ngati Iye sabwera, ndiye palibe chinthu chimodzi chimene ine ndingachite koma mwinamwake kuyambitsa mzere wa pemphero, kuyika manja pa odwala ndi kuwapempherera iwo, ndi kumapita kunyumba. Koma ndizo zonse zimene ine ndingathe kuzichita. Ine sindingathe. Ndine munthu. Ndine m’bale wanu. Mukuona?

²⁶⁴ Tsopano, koma tsopano ngati Mzimu Woyera ungachite chinachake chapamwamba, ndipo inu nkuganiza kuti ndi chopambana, Mulungu ndi chinthu chopembedzedwa, mupembedzeni Iye mochuluka momwe inu mungafunire kutero.

²⁶⁵ Koma, tsopano, ndipo musati muzitenga zithunzi, musati muzithwanimitsa kuwala, chifukwa Iko ndi Kuwala. Ndi

angati amene anayamba achiwonapo chithunzi cha Iko? Inu mukudziwa. Ndithudi. Icho chiri mu Washington, DC. Mukuona? Chabwino. Tsopano molemekeza.

²⁶⁶ Ndipo ine ndikanakonda inu amene muli kumbuyo kwanga mukanapemphera kwenikweni tsopano, chifukwa ine ndikuwawona omvetserawa, ndipo mwinamwake mawa usiku ine ndidzayesetsa kubwera mbali iyi, mwaona.

²⁶⁷ Tsopano, ine sindikudziwa. Ndi Mulungu yekha amene anapanga lonjezo. Koma ngati Iye ati adzizindikiritse Yekha apa, “Mabwana, ife tikufuna kumuwona Yesu,” ndipo ndiyo njira yokhayo imene inu. . . Inu simungatsanzire izo, chifukwa icho ndi—icho ndi chozizwitsa. Ndi chododometsa. Icho ndithudi ndi chododometsa. Mukuona? Chododometsa ndi chozizwitsa, chinachake chimene sichingakhoze kufotokozedwa.

²⁶⁸ Tsopano apa payima mkazi. Ine ndiribe lingaliro lirilonse kuti mkaziyo wayimira chiyani pamenepo monga wina aliyense amachitira, pokhapokha ngati pali winawake pano amene akumudziwa iye. Iye ndi mkazi chabe wayima pamenepo. Koma izo zachitika kuti ndi mkazi. Izo zikubwera mmalingaliro anga, chithunzi changwiwo cha Yohane Woyera 4, mwamuna ndi mkazi kukumana, monga Ambuye anakumana ndi mkazi pa chitsime. Mukuona? Tsopano, ngati dona uyu waima apa, ndipo ine osati. . . Iye akhoza kukhala kuti akudwala, mwinamwake iye sakudwala. Mwinamwake iye ali ndi vuto la pakhome. Mwinamwake iye ali ndi vuto la zachuma. Kapena mwinamwake iye wamuimirira apa winawake. Ine—ine—ine sindikudziwa chimene iye wabwerera pano. Ine basi sindingathe kukuuzani inu, chifukwa ine sindikudziwa. Ine sindikudziwa. Koma iye akudziwa.

²⁶⁹ Tsopano ngati ine ndikanabwera, monga, ndi kudzayika manja pa iye, ndi kuti, “Ine ndikuyika manja anga pa inu, mlongo. Ulemelero kwa Mulungu! Inu mukuyenera kukhala bwino, chifukwa Baibulo linati, ‘Ikani manja pa odwala, iwo adzachira.’ Ameni. Pitani pa njira yanu, mukusangalala. Inu mwachiritsidwa.” Chabwino, iye akufuna kuti akhulupirire zimenezo, izo ziri bwino, chifukwa ilo ndi Lemba, “Iwo adzayika manja pa odwala, iwo adzachira.” Izo ndi zooni. Icho ndi chimene Baibulo linanena.

²⁷⁰ Koma nanga bwanji ngati Mzimu Woyera utayima pano ndi kumuuzwa iye chinachake chimene iye wachita, chinachake chimene chakhala chiri mmbuyo pansu mmoyo wake, chimene iye wachita, chimene iye akuchita tsopano, chimene iye wadzera pano, chimene iye akufuna? Tsopano, ndiye iye adziwa, iye adziwa ngati icho chiri choonadi kapena ayi. Ndiye iye adziwa kuti zimenezo zikuyenera kubwera kuchokera ku mphamvu ina yauzimu. Tsopano izo zitengera chimene iye angafune kuchitcha icho, monga Bezezebule; kapena monga mkazi pa chitsime,

“Ife tikudziwa kuti Mesiya adzachita izi.” Mwaona, ndiye, chirichonse chimene icho chingakhale, imeneyo ndi mphotho yake imene iye angalandire.

²⁷¹ Komano ngati Iye angakhoze kumuza iye chimene iye wakhala ali, ndipo—ndipo ngati izo ziri zoon, iye azindikiritsa kuti izo ndi zoon. Ndiyeno ngati Iye angadziwe chimene iye wakhala ali, ndithudi iye akhoza kumudalira Iye pa chimene Iye anganene kuti iye adzakhala. Nkulondola uko? Ngati iye angamudalire Iye podziwa chimene Iye wakhala ali, iye adziwa ngati izo ziri zoon kapena ayi, ndiye nanga bwanji chimene Iye ati adzakhale?

²⁷² Kodi iyi si nthawi yopambana? Mukuti, “Kodi inu mukuchedwera chiyani, M’bale Branham?” Ine ndikumuyembekezera Iye. Ndizo ndendende, ndendende. Ngati Iwo subwera, ine sindingathe kuchita izo. Ndizo zonse, ine ndikungomuyembekezera Iye. Kulondola. Mukuona?

²⁷³ Tiyeni tiyimbe nyimbo yakale ija, *Kungo Khulupirira*. Tipatseni ife poyambira pamenepo.

Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira;
Kungo khulupirira, kungo khulupirira,
Zinthu zonse ndi zotheka, kungo khulupirira.

²⁷⁴ Tsopano, mu Dzina la Yesu Khristu, ine ndikuwutengera mzimu uliwonse muno pansi pa ulamuliro wanga, kwa ulemelero wa Mulungu. Tsopano khalani chete kwenikweni.

²⁷⁵ Tsopano, inu amene munachiwona chithunzi chimenecho, (ndipo ine ndidzakumana nanu tsiku lina pa Mpando Wachiweruzo wa Khristu), Iko sikuli mapazi awiri kuchokera pamene ine ndayima pakali pano. Uko nkulondola. Tsopano ngati umenewo uli Mzimu Woyera womwewo... Aliyense akudziwa kuti Mngelo wa Pangano anali Yesu Khristu, Amene anatogolera Israeli kudutsa mchipululu. Ndipo ngati Iye angabwere tsopano. Ndipo ine ndadzinenera kuti Iye ndi Kuwala kumeneko. Ine sindikudziwa basi kumene Iko kuli, koma Iko kuli pomwe pano pafupi ndi ine. Ine ndikukumverera Iko, ndipo ine ndikudziwa Iko kuli pano.

²⁷⁶ Tsopano ngati Iko kuti kuchotse moyo wanga, malingaliro anga omwe, kuzindikira za mumtima kwanga, chirichonse kutali ndi ine, ndi kubala Zake Zomwe, ndiye Uyo ndi Khristu. Tsopano kodi inu nonse mukhulupirira, ngati Iye ati achite zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino, tsopano khalani molemekeza kwenikweni. Ine ndikuyenera kuti ndiyankhule ndi donayu mphindi chabe.

²⁷⁷ Tsopano aliyense amene ali injiniya wa maikrofoni iyi apa, iwoneni iyo. Chifukwa, pamene iwe uli mmasomphenya, iwe uma—iwe uma—iwe umakhala kutali ndi kuno. Iwe umakhala kwinkwakwenso, pansi pa moyo wa munthuyo, kwinkwakwenso,

basi monga kukhala mu dziko lina, ndipo ndikuyenera kungoyankhula ndi kunena chimene ine ndikuchiyang'ana. Ndiyeno chifukwa icho chindichokera ine, ndipo zikatero sindimakumbukira chimene ndanena, mwaona. Kotero inu muwayang'ane maikrofoniwo, aliyense amene ali. Pamene ine ndikuyankhula ndi donayu chimodzimidzi monga momwe Ambuye wathu anachitira ndi mkazi pa chitsime, kungoyankhula ndi iye, kuti ndigwire mzimu wake.

²⁷⁸ Chifukwa, ine ndinayamba kulalikira, kanthawi kapitako, ndipo izo zinakhala ngati... Ine ndisanachoke mchipinda, pa tsiku, ine ndimasala kudya ndi kupemphera, ndipo Iko ndithudi kumakhala pafupi ndi ine. Ndipo ndimayenera ndingobwera mkati muno, kumulola winawake ayankhule, ndiyeno nkuyenda kupita pa guwa. Izo zimakhala zabwino kwambiri. Koma kungokhala pano usikuuno, ndiye ine—ine ndikufuna kuti ndiyankhule ndi donayo.

²⁷⁹ Tsopano, dona, Ambuye Yesu ndi wamkulu. Ndipo Iye si wakufa, koma Iye ndi wamoyo kwanthawizonse. Inue mukukhulupirira zimenezo? Ine—ine ndikukhulupirira kuti inu mukukhulupirira zimenezo. Tsopano ife tayima pano, ngati mwamuna ndi mkazi amene tikuyenera kudzakumana ndi Khristu tsiku lina, ife—ife tikuyenera kudzamuwona Iye. Koma ine ndazindikira kuti ndinu Mkhristu. Chifukwa, mwamsanga pamene ine ndiyamba kuyankhula, ndiye ine ndimamverera mzimu wawo ukubwera mkati.

²⁸⁰ Tsopano ngati donayo ati achitire umboni choona, pakali pano iye akumverera kumverera mwachirendo kwenikweni, ngati kukoma kwenikweni, kofunda. Tsopano ngati inu mungayang'ane ndi maso anu, inu amene simunakuwonepo Iko, apa Iko kuli pakati pa ine ndi iye, mwaona, kokhala ngati Kuwala kwa ambara. Iko kwakhazikika pa donayo, pakali pano. Ndipo, mu Dzina la Ambuye, iye akuzindikira kuti chinachake chikumupangitsa iye kumverera mokoma kwenikweni, mosiyana ndi chimene inu... .

²⁸¹ Basi, inu mukudziwa, kukhalapo kwa m'bale wanu sikukanakhoza kuchita zimenezo. Ngati izo ziri zoono, ingokwezerani mmwamba dzanja lanu kwa anthuwa. Mukuona? Eya.

²⁸² Tsopano pomwe pano, ine ndikuyang'ana pa donayo, kukhudzana kwangwiro ndi iye. Donayo akuvutitsidwa ndi chinachake, ndipo ndicho kuti ali ndi mthunzi. Pali mthunzi wakuda pa mkaziyo, ndipo iye akuvutika. Inde, ndi khansa. Iye ali ndi khansa, ndipo khansa imeneyo ili pa dzanja lake, pa chala chake. Uko nkulondola, pa dzanja lanu. Simungayiwo iyo apa, koma iyo ili pa dzanja lake, mulimonse. Uko nkulondola.

²⁸³ Nchifukwa chiyani izo, mosiyana, kuti winawake akuganiza... Musati, musayesetse kubisa malingaliro anu

tsopano. Ine ndikhoza kuwagwira iwo apa mwa Mzimu Woyera. Winawake anati, “Iye wangopeka zimenezo.” Ine sindinapeke zimenezo. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Tsopano, ine sindinapeke zimenezo. Ine sindinatero.

²⁸⁴ Chabwino, apa, inu basi...ine sindikutha kuyiwona iyo kuchokera pamene ine ndayima, iyo ili pa...

²⁸⁵ Apa, chabwino, ikani dzanja lanu pansi. Muyang’ane pa ine. Mundikhulupirire ine kuti ndine wantchito wa Mulungu. Kodi inu muchita zimenezo? Chabwino, tiyeni tipite kwinkwakwenso. Inde, ndinu wokhulupirira. Ndipo inu mukuyenera kukhulupirira chifukwa cha zimenezo. Ine ndinakupemphereranipo inu kamodzi, kalekale, ndi khansa, ndipo inu munachiritsidwa.

²⁸⁶ Inu mukuti, “Inu mukumudziwa mkaziyo.” Ine sindinatero. Ine sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga, momwe ine ndikudziwira, ndikungomuwona kokha iye mmasomphenya awa.

²⁸⁷ Pano ndiroleni ine ndikuwonetseni inu chinachake. Iye ali ndi winawake pa mtima wake, iye akumupempherera. Ameneyo ndi mwamuna wake. Iye ali pano. Ngati ine ndingakuuzeni inu lomwe liri vuto ndi iye, kodi inu mukhulupirira kuti iye achiritsidwa? Iye ali ndi vuto la thumbo. Ndipo ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Inde, Yesu Khristu wakuchizani inu.

²⁸⁸ Kodi inu mukukhulupirira? “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Kodi mukukhulupirira kuti Zimenezo ndi Mwana wa Mulungu? Tsopano ndi angati a inu mukukhulupirira kuti ndi Yesu Khristu? Mungokhala ndi chikhulupiriro. Musakayikire ayi. Mukhulupirire Mulungu. Iye ali basi wamkulu lero monga Iye analiri nthawizonse.

²⁸⁹ Tsopano inu munati, chimodzimodzi monga, “Mabwana, ife tikufuna timuwone Iye.” Tsopano, ngati izo zinamupangitsa mkazi pa chitsime, pansi pa chikhalidwe chimenecho, chake—chake—chikhalidwe chake chazimu, kuzindikira icho kukhala chizindikiro cha Mesiya; ndipo ife owerenga Baibulo, ndipo odzazidwa ndi Mzimu Woyera, kodi izo zikuyenera kuchita chiyani kwa ife?

²⁹⁰ Monga ine ndakhala ndikuganizira kawirikawiri kuti, pamene Maria pokhala ndi pakati pa Mzimu Woyera umene unamufungatira ndi kumulenga mwana uyu, unamuuya iye za zomwe zinkachitika. Iye anathamangira uko kuti akamuwone msuwani wake, Elizabeti, yemwe anali miyezi sikisi ndi—ndi Yohane, mkazi wa Zakariya. Ndipo iwo anali asuwani. Ndipo pamene Maria anamuuya Elizabeti kuti nayenso akanadzakhala ndi mwana, osamudziwa mwamuna, kuti Mzimu Woyera unali woti ukanadzamubweretsa iye, ndipo anati, “Iwo anamutcha Dzina Lake ‘Yesu.’” Inu mukudziwa, Yohane wamng’ono,

ndipo iye anali ndi miyezi sikisi m'mimba mwa amayi, ndipo iye anali asanasunthe nkomwe apobe. Mwaona, izo ndi zachilendo; pafupifupi miyezi iwiri kapena itatu ndipo mwanayo akusuntha. Koma, ichi chinali chachilendo, Yohane wamng'ono anali wakufa m'mimba mwa amayi ake. Ndipo mwamsanga pamene malonje a Maria anafika ku khutu lake, anati, "Ine ndidzamutcha dzina Lake, Yesu." Nthawi yoyamba imene Yesu Khristu anayamba watchulidwapo ndi milomo ya munthu, ilo linabweretsa mwana wamng'ono, wakufa ku moyo, m'mimba ya amayi ake.

²⁹¹ Kodi Ilo likuyenera kuchita chiyani kwa mwamuna kapena mkazi amene wabadwa mwa Mzimu wa Mulungu? Mukuona? Kodi Ilo likuyenera kuchita chiyani pamene ife tikudziwa kuti tikukhala mmasiku otsiriza, Lemba limene lawunjikidwa apa pathu—pakati pathu, usikuuno, pa maliwu athu kunja kuno, kumuwona Yesu Khristu akutipatsa ife chizindikiro chotsiriza moto usanabwere? Kodi Izo zikuyenera kuchita chiyani kwa ife? Kutitumiza ife ku maondo athu, ku kulapa.

²⁹² Ine ndikuyembekezera kwa mphindi chabe, ndithudi, kukhala ngati kudzisasa kuchoka kwa izo, chifukwa izo zimandifooketsa ine. Ngati izo zinamufooketsa Mwana wa Mulungu, ukoma unachoka mwa Iye, kodi izo zingachite chiyani kwa ine, wochimwa wopulumutsidwa mwa chisomo?

²⁹³ Tsopano apa pali mkazi wamng'ono monga... Kodi uyu ndi wotsatira, kodi uyu ndi... Inu muli bwanji? Ine ndinali nditatembenuka. Ine sindimadziwa. Ndife alendo kwa wina ndi mzake, ine ndikuganiza. Ife sitikudziwana wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu. Ndipo ndinu wa zaka zocheperako kuposa ine, ndipo ife mwinamwake tinabadwa mamailosi motalikana. Nthawi yathu yoyamba kukomana. Koma kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine mneneri wa Mulungu, kapena, mundikhulukire ine, ine ndikutanthauza wantchito wa Mulungu? Izo zimawapunthwitsa anthu, chifukwa... Izi ziri pa tepi. Kodi inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake?

²⁹⁴ Kodi inu mukukhulupirira kuti Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse? Ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti, inu, Kuwala uku kumene ine ndikukukamba, kuti umenewo ndi Mzimu wa Mulungu, Mzimu womwewo, Lawi la Moto lija limene linadutsa mchipululu ndi ana a Israeli, linawonetseredwa? Mmodzi yemweyo amene anabwera mu ndende usiku umenewo, Kuwala kuja, ndi Simoni Petro, ndipo kunatsegula zitseko za ndende, kunamutulutsa iye, mfulu?

²⁹⁵ Kodi inu mukukhulupirira kuti tsiku lina Iye adzabwera ndi kudzatipanga ife afulu? Ine ndikutero, nanenso. Adzabwera ku manda ndipo adzatsegula zitseko, ine ndidzatuluka kuchoka

pakati pa akufa. Ine ndikumudalira Iye. Iye ali pano usikuuno. Kodi izo si zodabwitsa kudziwa kuti ife sitikusowa kutenga mbalume zina za umunthu? Ife tiri ndi Baibulo apa limene likuyankhula za izi. Ndipo apa Iye ali woti awuzindikiritse Mpingo Wake, kuti awupatse iwo chikhulupiro chokwatulitsa kuti uchotsedwepo. Munthu angakhale bwanji phee!

²⁹⁶ Ndikungoyankhula ndi donayu. Tsopano, ine sindikumudziwa iye. Dzanja langa ndi ili, ine sindinamuwonapo iye, momwe ine ndikudziwira. Basi, ngati ine sindikukudziwani inu ndipo inu simukundidziwa ine, kuti anthu anene. . .

²⁹⁷ Winawake ananena, bambo uja amene ndimayankhula naye lero, kumusi uko ndikutola zanzitini, iye ananena, kuti, “Anthu amati, ‘M’bale Branham amabweretsa gulu lake lomwe ndi iye, umo ndi momwe iye amawadziwira iwo.”

²⁹⁸ Ine ndikulumbira mwaulemu pamaso pa Mulungu, ine sindinayambe ndamuwonapo mkazi ameneyo mmoyo wanga, momwe ine ndikudziwira, kapena palibe wina aliyense mu mzere umenewo.

²⁹⁹ Ngati ife tiri mwamtheradi alendo kwathunthu, mlongo, ine sindikukudziwani inu kapena kalikonse ka inu, kwezani mmwamba dzanja lanu, ngati ine sindikukudziwani inu ndipo inu simukutero. Ndi zimenezotu pamenepo. Ine sindinayambe ndamuwonapo mkaziyo. Chabwino.

³⁰⁰ Koma ine ndikumudziwa Winawake wayima pano ndi ife, Yemwe akutidziwa awiri tonse a ife, Iye watidyetsa ife masiku onse a moyo wathu. Ndi Iyeyo yemwe ine ndimamudalira. Ndi Iyeyo yemwe ine ndimamukhulupirira.

³⁰¹ Tsopano ngati ine ndingakuthandizeni inu, ndipo nkusachita icho, ine sindikanakhala woyenera kuyankhula za Mawu awa. Ine siwoyenera ayi, mulimonse. Koma ngati ndingathe kukuthandizani inu, ndipo nkusachita izo, koma chinthu chokhacho chimene ine ndingathe kuchita. . .

³⁰² Ngati Iye akanayima pano, ndipo inu nkukhala mukudwala, inu mukanati, “Yesu, ndichiritseni ine.” Iye akanati, “Ine ndinachita kale izo pamene ine ndinafa pa Kalvare.” Iye *anavulazidwa* chifukwa cha zolakwa zathu. Apo mtengowo unalipiridwa, izo zinathetsedwa.

³⁰³ Koma tsopano Iye akhoza kutsimikizira kuti Iye anali Yesu, pokuwonetserani inu chizindikiro cha Umesiya, kuti Iye anali Yesu. Ndipo Iye analonjeza kudzachita izo. Chiyani. . . Mai! Palibe potseguka basi poti mdierekezi angathawirepo, ndi choncho? Iye wayikidwa pakona. Kodi Iye si wodabwitsa? Ine ndikufuna. . .

³⁰⁴ Chifukwa chimene ine ndimanenera zimenezo, ine ndikuwona chinachake chikuchitika. Donayo wangobwera kumene kuchokera ku opareshoni. Uko nkulondola. Nkulondola

uko? Vuto lachikazi, ndipo inu munali ndi oparesoni. Inu muli... Nkulondola uko? Ndipo inu mukuvutika ndi kufooka kwenikweni ndi manjenje. Si kulondola uko? Simukutha kuchira ku zimenezo. Ndipo inu mwabwera. Ndipo usikuuno, musanabwere, inu munapemphera kuti inu mukhoze kufika kuno ndi kudzapemphereredwa, mu mzere. Nkulondola uko? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Ine sindikuwerenga malingaliro ake. Ayi, ayi. Ngati ine nditakuuzani inu yemwe inu muli, mwa Mzimu wa Mulungu, inu mudziwa ngati izo ziri zoon kapena ayi, sichoncho inu? Kodi izo zingakupangitseni inu kukhulupirira? Kodi inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Akazi a Gideon, mukhulupirire. Uko nkulondola. Pitani kwanu, Yesu Khristu wakuchizani inu. Ndipo mukhulupirire.

³⁰⁵ Kodi inu mukukhulupirira? Tiyeni tinene, “Ambuye alemekezeke.” [Osonkhana akuti, “Ambuye alemekezeke.”—Mkonzi]. Mai, kalanga, chiyani... Mungokhala ndi chikhulupiro mwa Mulungu. Musakayikire.

³⁰⁶ Kumbukirani, zimenezo zinali PAKUTI ATERO AMBUYE. Penyani zimene Iye akunena. Mukuona? Masomphenya ndi chinthu chimodzi, ndipo PAKUTI ATERO AMBUYE ndi chinanso.

³⁰⁷ Inu muli bwanji, bwana? Ndine mlendo kwa inu. Ndife a mitundu iwiri yosiyana, ngakhale; monga mkazi uja anali pa chitsime, koma Yesu anamudziwitsa iye. Mulungu anapanga a magari amodzi anthu onse. Mafuko ndi malo kumene ife tinaleredwerako, ndi kusintha mitundu yathu, ziribe kanthu kochita ndi ife. Ndife abale, zolengedwa, tonse tinabwera kuchokera kwa Adamu. Uko nkulondola. Koma mitundu iwiri yosiyana yakumana pano usikuuno, chimodzimodzi monga izo zinachitikira nthawi imeneyo. Ngati Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, akhoza kuwulula kwa ine chimene mukuchifuna mwayimira pamenepo, kodi inu mukukhulupirira kuti Iye angapereke icho kwa inu? Inu mukuchidziwa chimenecho. Zikomo inu, bwana. Inu mukudziwa zimenezo. Chabwino, ndiye vuto lanu la mmimba likusiyani inu, ndipo matenda anu a shuga akhala atapita. Bwererani kwanu.

“Ngati inu mungakhulupirire, zinthu zonse ndi zotheka.”

³⁰⁸ Tsopano aliyense akhoza kuwona, akumuthandizira iye pamwamba apo, pali chinthu chinachake cha ulumali mwa iye. Ine sindikudziwa. Ine sindinamuwonapo mkaziyo. Iye ndi mlendo kwathunthu. Ngati ndingakhoze kumuchiza iye, ine ndikanachita zimenezo. Ine sindingathe. Tsopano yang’anani mbali iyi, mlongo. Petro ndi Yohane... uko ndi kungogwira... Mwaona, pali anthu pozungulira, inu mwaona. Kumbukirani Iye akumutsogolera munthu wakhungu kunja kwa mzinda, ndi zina zotero, mwaona, akupita kwa Iyemwini. Mwaona, munthu aliyense ndi mzimu wamoyo, mwaona, ndipo Iwo uyenera

kukuchotsani inu kuchokera ku chikhulupiro kuchokera kulikonseko.

³⁰⁹ Tsopano, ine sindingathe kuchiritsa. Inu mukudziwa zimenezo. Ndine munthu, chimodzimodzi monga anu—amuna anu angakhalire, abambo anu, kapena wina aliyenseyo. Ndine munthu, munthu chabe. Koma Iye ndi Mulungu. Uko nkulondola.

³¹⁰ Tsopano, ndi zoonu kuti kulumala kwanuko ndi nyamakazi. Ndipo inu—inu muli ndi nyamakazi. Iyo ndi yoipa, ikuyipirayipirabe nthawi zonse. Uko nkulondola. Ndipo chinthu china, inu muli ndi vuto lalikulu lamanjenje. Inu muli ndi vuto la chikhodzodzo. Uko nkulondola. Kuthamanga kwa magazi. Mwangokhala ndi zosokonekera. Uko nkulondola. Sindinu wochokera kuno. Ayi, inu mwabwera kuchokera ku California. Inu mubwereranso, ndipo mukhulupirire. Inu mukhala bwino, mu Dzina la Yesu Khristu. Mukhale ndi chikhulupiro.

³¹¹ Inu mukukhulupirira? Chabwino, tiyeni tingokweza mmwamba manja athu ndikuti, “Zikomo Inu, Ambuye Yesu.”

Ndipo, Ambuye Yesu, ife tikukupatsani Inu matamando ndi ulemelero, chifukwa cha ubwino Wanu wonse ndi chifundo kwa ife. Mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

³¹² Ingokhalani ndi chikhulupiro ndipo mukhulupirire. Tsopano tayang’anani pa iye akupita. Tayang’anani pamenepo. Mukuona? Mukuona? Nenani, “Ambuye alemekezeke.” [Osonkhana akuti, “Ambuye alemekezeke.”—Mkonzi]. Amen.

³¹³ Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye samanama. Iye amanena zoonu. Chimene Iye amakuuzani inu, icho chimakhala mwanjira imeneyo basi. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye samalephera konse.

³¹⁴ Tsopano, aliyense amene akukhulupirira zimenezo, ngati inu mungavomereze izo, izo zichita chinthu chomwecho pa inu. Chinthu chokhacho chimene inu mukuyenera kuchita ndi kukhulupirira. Tsopano, aliyense mwa omvetsera akukhulupirira? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino.

³¹⁵ Nanga bwanji inu ndi mitsempha yotupa imeneyo? Inu mukuganiza kuti Mulungu angakuchizeni inu kwa iyo, kukupangani inu kukhala bwino bwino? Kodi inu mukukhulupirira? Chabwino, iyo ikusiyani inu ndiye.

³¹⁶ Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu, “Ndani, kodi iye anakhudza Ndani?” Iye sanandikhudze ine. Nkulondola uko?

³¹⁷ Nanga bwanji inu, kodi inu mukukhulupirira? Inu mukukhulupirira kuti ululu umenewo kumbali yanu uchoka? Inu mukuvutika ndi ululu kumbali yanu. Chabwino, iwo uchoka.

³¹⁸ Ine ndikukubetcherani inu kuti mukhulupirire izo, Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, akudzizindikiritsa Yekha pakati pa anthu Ake. Ine sindinamuwonepo mkazi ameneyo, sindinamuwonepo munthu ameneyo. Kodi iwo anakhudza chiyani? Iwo anamukhudza Wansembe Wamkulu. Iwo ali mapazi twente kuchokera kwa ine. Iwo sangathe kundikhudza ine; sizingachite ubwino uliwonse, mulimonse. Koma iwo anamukhudza Wansembe Wamkulu, ndipo Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Iye ndi Yesu Khristu. Inu mukuyenera kukhulupirira, chonchobe.

³¹⁹ Tsopano munthu uyu, apa pali mwamuna, monga Simoni Petro. Mwinamwake mwamuna woyamba amene wabwera usikuuno, ine ndikukhulupirira. Mwamuna wabwera pano, monga Ambuye Yesu; mwamuna, Simoni Petro anabwera pamaso pa Ambuye Yesu. Mwamuna; ine ndikuganiza kuti akhala ali akazi, tsopano ndi mwamuna. Tsopano ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, ndiye Iye akhala basi monga Iye anachitira nthawi imeneyo. Nkulondola uko? Tsopano ine sindikumudziwa bamboyo; Atate Akumwamba akudziwa zimenezo. Ine sindikumudziwa iye. Iye ndi munthu chabe wayima apa. Koma Yesu Khristu akumudziwa iye. Ndipo ngati Yesu Khristu angawulule kwa ine chimene iye wabwerera pano, kapena chinachake chokhudza iye, ndipo—ndipo Iye nkuchiyankhula icho, iye adziwa ngati izo ziri zoonza kapena ayi. Bamboyo adziwa zimenezo. Ndipo ngati aliyense pano akumudziwa iye, iwo adziwa zimenezo. Koma ine—ine sindikuzidziwa zimenezo. Ine ndikungoyenera kuti ndidikirire. Koma yankho liri pano. Ilo liri pano, liri mwa Khristu. Uko nkulondola, ndipo ife tikuzikhulupirira zimenezo.

³²⁰ Ndipo tsopano iyi ndi nkhani yofooketsa; kwambiri, yofooketsa kwambiri. Ndipo ine ndikudalira kuti inu mukhulupirira ndipo mukhala ndi chikhulupiriro.

³²¹ Tsopano, posakudziwani inu, bwana. Ndipo chimodzimodzi monga momwe winawake anamubweretsera Simoni pamaso pa Ambuye Yesu. Tsopano ine sindikunena kuti . . . Ine si Ambuye Yesu, mwaona. Ndine munthu chabe. Koma ine ndikuyesetsa kunena kuti Iye ali pano pakati pa anthu, ndipo ine ndikufuna kuti iwo awone. Ndipo ngati iwo angathe kuziwona izo, ndiye ndithudi iwo—iwo akhoza kukhulupirira ndi kuvomereza izo. Pamene zonse . . . Ngati lonjezo ili, ngati Iye angapange . . . Iye sangathe kungobwera kunja uko, ndi kulowa muno, nkuti, “Ine ndikuchiritsani *inu*. Ine ndikuchiritsani *inu*.” Ake . . . Izo zingakhale zotsutsana ndi Mawu Ake. Mwaona, Iye anachita kale zimenezo. Iye ali basi . . .

³²² Chinthu chotsiriza chimene Iye angachite ndi kungotsimikizira kuti Iye ali pano kuti asunge Mawu Ake. Ndipo ngati Iye ati asunge izi ndi kuziwonetsera izo pamwamba pano pamaso pa anthu nonsenu, ndithudi mkazi wolumala uja amene

amayenera ngakhale kukwezedwa pa chinthu cha mainchesi foro pamenepo, ali ndi nyamakazi, analumpha mmwambandi-pansi ndi kuthamanga kudutsa apa, chifukwa izo zinali PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona? Iye anamuchiza iye. Tsopano ndithudi inu mukhoza kukhulupirira kuti Iye ali pano.

³²³ Tsopano munthu uyu, mlendo kwa ine, ndipo ine kwa iye. Ndife tonse awiri alendo. Tsopano ngati Ambuye Yesu ati awulule izo, mulole iye akhale woweruza. Ndiye kodi inu nonse mukhulupirira ndi kulandira machiritso anu, chirichonse chimene, kodi inu mukhulupirira ndi zonse . . .

³²⁴ Dona wina anawonekera pano patsogolo panga. Donayo apo ali ndi vuto la mapapo, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse ndipo Yesu Khristu akuchizani inu, ngati inu mungathe kukhulupirira. Inu mukukhulupirira zimenezo? Ndine mlendo kwa inu, koma Yesu Khristu akudziwa chimene inu mukuganiza. Tsopano inu mukhulupirire, ndipo inu mukhala bwino. Amen. Amen.

³²⁵ Kodi Iye si wodabwitsa? Ine sindikumudziwa mkaziyo, sindinayambe ndamuwonapo iye mmoyo wanga. Iye ndi dona chabe wakhala pamenepo. Koma iye . . .

³²⁶ Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake. Iye anali atakhala pamenepo, akuti, “Ambuye, ndiloleni ine ndikukhudzeni Inu.” Mufunseni iye ngati izo si zoon. Ndi zimenezotu. Uko nkulondola.

³²⁷ Ndipo ine ndinamuwona iye akuwonekera apa, ndipo ndinamva chimene iye ananena, ndipo ndinayang’ana mmbuyo, ndipo ine ndinaganiza, “Alikuti munthu wa mawonekedwe oterowo?” Ine ndimalephera kuziwona izo paliponsepo. Ndipo ine ndinapitirira kuyang’ana. Ndipo pamene iye amakhoza . . . Ine ndinayang’ana pozungulira, molunjika ine ndinawona Kuwala kuja kukusuntha apo ndipo kunadzapachikika pa mkaziyo, apo iye anali, mwaona. Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Amen. Ambuye Yesu amadziwa chirichonse.

³²⁸ [M’bale akuti, “Donayo anabwera ndi ine.”—Mkonzi]. Icho ndi chimene icho chinali. Bambo uyu akuti donayo anabwera ndi iye. Amen. Kodi icho si chinachake? Mukuona? Tsopano kodi . . . Kodi izo si zodabwitsa? Ambuye Yesu amadziwa zinthu zonse. Kodi inu simukuwona? Ameneyo sangakhale ine, abwenzi. Inu mukudziwa zimenezo. Ndinu—ndinu aluntha kwambiri kuposa zimenezo. Inu mukudziwa zimenezo.

³²⁹ Tsopano kwa munthu uyu wayima apa. Tsopano, posakudziwani inu, ndipo osadziwa kanthu za inu, ngati Ambuye Yesu angawulule kwa ine chinachake chimene inu mwabwerera pamenepo, kapena chinachake chimene inu mwachichita kuti chiyambitse vuto lanu, kapena chirichonse chimene icho chiri, ndiye inu mudziwa kuti Iye, izo zikuyenera

kukhala Ambuye Yesu. Uko nkulondola. Chabwino, tsopano mulole Iye apereke izo.

³³⁰ Chinthu choyambirira, munthuyo akuvutika ndi—ndi vuto la magazi. Ayi, ndi kuthamanga kwa magazi. Iye akuvutika ndi kuthamanga kwa magazi. Iye alinso ndi chinachake cholakwika ndi thupi lake. Ine ndikumuwona iye atakhala ali ndi mapazi ake mmwamba, kapena ena. . . Oh, ndi—ndi madzi akusonkhana mozungulira mmapazi anu, mozungulira monga choncho. Mukuti, ndinu mtumiki, mlaliki wa Uthenga. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kundiuza ine yemwe inu muli? M’busa Williams, ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kuchoka pano ndi kukakhala bwino. Mulungu akudalitseni inu. Amenii.

Kodi inu mukukhulupirira?

³³¹ Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza khansa? Kodi inu mukukhulupirira kuti Iye amachiza khansa ndipo amawachiritsa anthu? Pitirirani kuchoka pa nsanja, mukukhulupirira, ndipo mukachiritsidwe. Amenii. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

³³² Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu amachiza vuto la mtima? Inu mukutero? Chabwino, ndiye wanuwo wachiritsidwa. Pitani ndipo mukakhulupirire ndi mtima wanu wonse. Basi matamando akhale kwa Mulungu! Amenii.

³³³ Tsopano, inu munali ndi kumverera kwachirendo kwenikweni pamene ine ndinanena zimenezo kwa bamboyo, chifukwa inu munali ndi vuto la mtima, nanunso. Ngati inu muti mupitirize kukhulupirira, ilo silibwereranso. Ilo likusiyani inu kotheratu. Pitani, mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Amenii. Chabwino.

³³⁴ Mkazi uyu akubwera apa ali ndi mthunzi wa imfa. Iye anali ndi khansa, koma tsopano iyo yapita. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse, ndipo iyo ipita, ndipo muchiritsidwe. Ngati inu simukayikira, iyo sidzabwereranso konse ngati inu simukaikira zimenezo, koma mukhulupirire.

Bwerani, dona.

³³⁵ Tsopano inu mukuti ine ndinali “kuwerenga maganizo a anthu.” Zitembenuzeni izo monga chonchi. Mngelo wa Ambuye amene ankayenera kuti abwere mmasiku otsiriza, Ambuye Mulungu Yehova, ankayenera kudziwa chimene chinali kumbuyo Kwake, monga Iye anachitira. Mkazi uyu ali kumbuyo kwanga.

³³⁶ Mukukhulupirira, mlongo. Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito wa Mulungu? Ngati inu mukutero, kwezani mmwamba dzanja lanu.

³³⁷ Dona uyu kumbuyo kwanga, kodi iye wakweza mmwamba dzanja lake? [M’bale akuti, “Inde.”—Mkonzi]. Ngati Ambuye

angawulule kwa ine, ndikuyang'ana mbali *iyi*, chimene chiri cholakwika ndi mkaziyo, kodi inu mukhulupirira ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana akuti, "Inde."] Iye ali ndi vuto lachikazi, vuto la chikazi.

³³⁸ Ngati uko nkulondola, gwedezani dzanja lanu, dona uyu apa. Inu mwachiritsidwa tsopano, ndipo Yesu Khristu wakuchizani inu. Ulemelero kwa Mulungu! "Monga izo zinali mmasiku a Sodomu, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu."

³³⁹ Malo awa pa nkhope yake asanduka khansa. Ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupita, ndipo iyo ikusiyani inu, ndipo inu mukakhala bwino. Ine sindingathe kukuchizani, koma Mulungu atero ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse. Ine si mchiritsi. Uh-huh. Amen.

³⁴⁰ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse?

³⁴¹ Yang'anani mbali *iyi*, dona. Inu mumavutika ndi nyamakazi, iyo imavuta kwambiri mmawa, pamene inu mukuyesera kuti muchoke pa bedi. Mumatulutsa phazi limodzi kunja, ndipo kenako nkumayesera kupanga njira yanu, ndipo mumagwira zinthu nthawizina, mnyumbamo, kuyesetsa kuti muyende chozungulira. Uko nkulondola ndendende. Ngati inu mungakhulupirire ndi mtima wanu wonse, Yesu Khristu akuchizani inu. Mawa masana zidzakhala zosiyana, ngati inu muti mukhulupirire izo.

³⁴² Tiyeni tinene, "Ambuye alemekezeke." [Osonkhana akuti, "Ambuye alemekezeke."—Mkonzi].

³⁴³ Bambo uyu ndi wachikulire. Iye ali ndi vuto lotchedwa thumbo, umene uli usinkhu wa umunthu wake. Iye ali ndi zinthu zambiri zolakwika ndi iye. Koma chimodzi cha zinthu zazikulu chimene iye akufuna kuti ine ndimupempherere iye, ndi nyamakazi. Yakhala ikumusautsa iye kwa nthawi. Uko nkulondola. Kodi inu mukukhulupirira? Pitani pa njira yanu ndipo mukachiritsidwe. Ndipo mumuthokoze Yesu Khristu, amachiritsa odwala! . . . ? . . . Chabwino, bwana.

³⁴⁴ Ine sindikumudziwa mtsikana wamng'onoyo, mwana wooneka wathanzi. Tayang'ana pa ine ndipo ukhulupirire, dona. Kodi iwe ukhulupirira ndi mtima wako wonse? Kodi iwe ukundikhulupirira ine kukhala wantchito Wake? Kodi iwe ukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwulula kwa ine vuto lako? Iwe wangotsala pang'ono kusweka, chifukwa cha chikhalidwe cha manjenje. Mdierekezi wakunamiza iwe, akuyesetsa kuti akupangitse iwe kumaganiza kuti ukusokonezeka mmalingaliro ako, ndi chirichonse. Usakhulupirire zimenezo. Ndiwe mfulu. Yesu Khristu wakupanga iwe mfulu. Amen.

³⁴⁵ Kodi inu mukukhulupirira, omvetsera nonsenu? Kodi inu mukukhulupirira tsopano, mu Kukhalapo Kwake?

³⁴⁶ Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, mlongo? Kodi inu mukumukhulupirira Iye? Inu mukutero? Mu Dzina la Yesu Khristu, muchiritsidwe. Ameni. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

³⁴⁷ Iye ali ndi wamanjenje, ali ndi vuto la udona, nayenso akuvutika ndi nyamakazi. Iyo yatsala pang'ono kumulumalitsa iye. Ngati inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kupita kukakhala mfulu. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndiye, zipitani mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu. Ine ndikukhulupirira kuti iye wawongoledwa, ndipo wachiritsidwa.


³⁴⁸ Kodi inu mukukhulupirira ndi mitima yanu yonse? Tsopano dikirani. Kodi Yesu Khristu amasunga Mawu Ake? Kodi Iye amasunga Mawu Ake? Ndi angati akukhulupirira kuti Iye ali yemweyo? Ndi angati mukukhulupirira kuti inu mukumuwona Yesu Khristu akugwira ntchito pakati pa anthu Ake? “Mabwana, ife tikufuna timuwone Yesu.”

³⁴⁹ Tsopano, ine ndikukuuzani inu choonadi. Basi ndithudi inu mukhoza kukhulupirira ngati Mulungu akukuuzani inu kuti ine ndikukuuzani inu choonadi. (Tsopano ine ndikumverera mwana wanga kapena winawake akukoka pa chikhotho changa, chimene chikutanthauza kuti ndi nthawi yoti iye andilole ine kuti ndizipita.) Ine ndikufuna ndikuuzeni inu choonadi, amenewo ndi Mawu a Mulungu olonjedwa kuti adzachite zimenezo.

³⁵⁰ Mawu nawonso analonjeza izi. Inu munakweza mmwamba manja anu ndipo munati inu munali okhulupirira. Nkulondola uko? Mawu otsiriza amene Yesu ananena, Iye asanakwere Mmwamba, Iye anati Iye anapereka mphatso kwa anthu, Iye anati, “Zizindikiro izi zidzawatsatira iwo amene akhulupirira. Ngati iwo adzayika manja awo pa odwala, iwo adzachira.” Nkulondola uko? “Ngati iwo,” okhulupirira.

³⁵¹ Ndi angati ali okhulupirira, nenani, “Ameni.” [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndiye muyike dzanja lanu pa winawake pafupi ndi inu. Mungoyika dzanja lanu pa amene ali pambali panu. Mungoyika dzanja lanu pa wina ndi mzake. Oh, tsopano mumupempherere munthu ameneyo.

Ambuye Yesu, perekani izi, Ambuye.

³⁵² Satana, tuluka mu gulu ili la anthu, mu Dzina la Yesu Khristu. 

63-0627 Yesu Khristu Yemweyo
Dzulo, Lero, Ndi Kwanthawizonse
Associated Brotherhood Of Christians Campground
Hot Springs, Arkansas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org